# ISRAELI NDI MPINGO 4

Mu Bukhu la Numeri, ife tinatsegulako usiku wathawu, ife takhala tiri ndi masiteji anayi, masiteji atatu a ulendo, kutenga sabata ino, ya umwendamnjira wa ana a Israeli, choyimira, monga ife timakhulupirira mu kufanizitsa, kufanizitsa Mpingo Wakale ndi Watsopano; iwo mwa chirengedwe, ife mu uzimu. Ambuye wakumana nafe ife.

2 Ife tinabwereranso mwa Abrahamu, Isaki, Yakobo, Yosefe; mpaka mmusi mu ukapolo ku Igupto.

3 Ndiye usiku wathawu Ambuye anatidalitsa ife ndipo ife tinawatulutsa iwo, mpaka ku Nyanja Yofiira, mpaka ku Thanthwe lokanthidwa, uko atayima pamaso pa Mulungu.

4 Tsopano, usikuuno ife tikuwatengera iwo ku Kadesi-barnea, mpaka ku mpando wachiweruzo pamaso pa guwa la mkuwa, kapena njoka ya mkuwa, kani.

5 Mawa usiku, Ambuye akalola, ife tidzawatengera iwo ku dziko la kwawo. Oh, mai! Kutuluka, ife tidzawoloka Yordano mawa, Ambuye akalola. Yoswa anawauza iwo, anati, "Dzisonkhanitseni pamodzi tsopano, ife tikufuna tiwoloke." Tsopano basi asanati . . .

6 Inu mukudziwa, palibe aliyense wa ife koma, kapena mtumiki aliyense, koma amene ali ndi Mulungu pa mtima wake, koma pamene iye ayang'ana pa Malemba iye—iye basi amangokhala ndi mantha pang'ono, "Kodi ine ndikupita pa izo mwa ine ndekha, kapena kodi Mzimu Woyera uli pano kuti unditsogolere ine?"

7 Kumbukirani, kuti mbewu imene yafetsedwa, iyo mosakayika idzagwira penapake, ndipo ife tikufuna kuti iyo ikhale Mbewu ya Mulungu yeniyeni yowona yosaipitsidwa yomwe yafetsedwa mu mtima wa anthu, pakuti tsiku lina ine ndidzakaima mu chiweruzo kudzayankhira pa zomwe ine ndanena ndi kuchita mmoyo uno, limodzi ndi inu. Ngati ine ndikusocheretsa, ndiye ine ndidzawerengedwa wo—wosocheretsa. Ndipo ine ndithudi sindikanafuna kuchita zimenezo, osati mwadala.

8 Basi ife tisanakhale ndi pemphero, kapena ife tisanakhale ndi pemphero pa Mawu. Inu mukudziwa, Baibulo linanena kuti pamene Yohane anawona izo mu Bukhu la Chivumbulutso, iye anati iye analiwona Bukhu, ndipo Ilo linali losindikizidwa kumbuyo, kutsogolo ndi kumbuyo, ndipo palibe munthu Kumwamba, ndipo kunalibe munthu pa dziko lapansi, kapena kunalibe munthu kupansi kwa dziko lapansi, anali woyenera kuti alitenge Bukhulo kapena ngakhale kuyang'ana

pa Ilo. Ndiyeno Mwanawankhosa amene anali ataphedwa kuyambira makhazikitsidwe a dziko lapansi, anabwera, ndipo anadzalitenga Ilo kuchokera mdzanja la Mmodzi amene anakhala pa Mpandowachifumu. Ndipo akulu anafuula, “Ndinu woyenera!” Tsopano mulole Mwanawankhosa ameneyo usikuuno abwere ndipo adzatsegule Mawu. Ife tikhoza kusanthula masamba, koma zimatengera Mwanawankhosa wa Mulungu kuti atsegule Mawu.

9 Kodi ife tingaweramitse mitu yathu. M’bale Junior, titsogolereni ife mu mawu a pemphero, ngati inu mungathe, pamene tikupemphera kuti Mulungu atsegule Mawu Ake kwa ife, ngati inu mungathe. [M’bale Junior akupemphera—Mkonzi]. Chabwino. Ambuye akudalitseni inu tsopano.

10 Titembenuzire, kuti tiyambepo, usikuuno, ku Numeri, mutu wa 13. Ife tiyambira pamenepo, ndipo kenako ife tizitsatira. Basi ine ndiyesetsa kuti ndisachite monga ine ndakhala ndikuchitira, kukusungani inu nthawi yayitali, koma ine...tsopano ndikulolani inu muzipita mwamsanga basi. Mwamsanga pamene Mzimu Woyera udzati zakwanira, ndiye ife tidzakhala tikupita.

11 Mawa mmawa, tsopano kumbukirani, Sande sukulu, hafu-pasiti naini. Ndipo isanafike, kapena podzafika teni koloko, ife tidzakhala tikuyankha mafunso. Mubweretse mafunso anu, muwabweretse iwo usikuuno. Ukatha utumiki, mudzawapereke iwo kwa ma eledara ena kuti ine ndidzakhoze kuwatenga iwo, kapena mwanjira ina, kwa mafunso mawa. Ndiri nacho chiwerengero chabwino cha iwo.

Mawa usiku, ndi Kuwoloka Yordano.

12 Tsopano, ife takhala nawo masiteji atatu. Alipo masiteji atatu aulendowu: Israeli mu Igupto; Israeli mu chipululu; Israeli kudziko lakwawo, Palestina, wolonjezedwa ndi Mulungu zaka mahandiredi ambiri mmbuyomo.

13 Chabwino, ife tikupeza ndiye, tikuwutengera mpingo mmbuyo kuti tingokhala ndi kuwoneratu pang’ono, tinapeza kuti Mulungu anamulonjeza Abrahamu kuti Iye akanadzamupulumutsa iye, anamupatsa iye lonjezo lopanda mangawa, pangano lopanda mangawa. Iye akanadzamupulumutsa iye ndi Mbewu yake; osati mbewu yake yonse, koma Mbewu yake yolonjezedwa, (Isaki). Abrahamu anali ndi ana aamuna leveni, inu mukudziwa, koma Mmodzi yekha wa iwo anali Lonjezo, kudzera mwa Isaki. Ndi chifukwa chake Paulo ananena, mu—mu Aroma, mutu wa 9, kuti “onse amene ali Israeli si Israeli, koma kudzera mwa Isaki Mbewu idzaitanidwa.” Tsopano, ndiye Mulungu, kudzera mwa Isaki, kuyimira Khristu.

Ife tikuzindikira, Khristu anali mwa Abrahamu, Khristu anali mwa Isaki, Khristu anali mwa Yakobo, Khristu anali mwa Yosefe, Khristu anali mwa Mose.

14 Khristu ali mu Chipangano Chakale chonse, mu Chipangano Chakale chonse. Chonsecho... Ngati ife tikanakhala ndi nthawi! Kuno zaka seveni zapitazo, sabata yatha iyi... Miyezi ingapo yapitayi ife tinatenga Bukhu la Eksodo, kuchokera mbali imodzi kupita ku imzakeyo, kuyimira chirichonse. Ngakhale madzi olekanitsa; ng'ombe yamphongo yofiira, iyo siikanakhoza kukhala yabulauni, iyo inkayenera kukhala yofiira; yopanda dontho pa iyo. Iyo inkayenera kuwotchedwa. Ndipo kenako nkupangidwa kukhala madzi olekanitsa, ndipo ndi oti azikonkhedwa anthu iwo atatha kuchimwa ndipo amatuluka kunja kwa msasa. Momwe hisope, ndi mtengo wa mkungudza, ndipo zonse zitasakanizidwa pamodzi, momwe nkhuni mu chihema, momwe guwa la mkuwa, mtsuko, mkate wopanda chotupitsa, chirichonse chinkalozera kwa Khristu. Ndipo mwa Iye ndife amphumphu, mwa Yesu Khristu.

15 Tsopano, momwe phunziro lathu liliri lodabwitsa usikuuno, momwe Mulungu anamubweretsera Israeli ngati choimira, kuchitira mthunzi chimene chikanati chidzakhale.

16 Tsopano, ife tikupeza ndiye, iwo, zitatha zaka foro handiredi, Mulungu anali atamulonjeza Abrahamu kuti mbewu yake idzakhala mlendo mdziko lachilendo kwa zaka foro handiredi, koma adzatuluka pansi pa dzanja lamphamvu. Malonjezo a Mulungu nthawizonse amakhala owona. Mulungu nthawizonse amapangitsa Mawu Ake kukhala olondola. Magudumu akale aulosi ndi zimano za Mulungu zikupera pang'onopang'ono, koma motsimikiza, zikufika mpaka pa malo.

17 Ndi chifukwa chake usikuuno, powerenga eksodo iyi ya mpingo, ine ndikukhulupirira kuti ife tiri mu eksodo kachiwiri. Ine ndikukhulupirira, Mose pokhala choyimira changwiro cha bungwe la mpingo limene linamulephera Mulungu, ndi Yoswa watsopano—mtsogoleri watsopano; akuyimira, mpingo mu kulephera kwawo kwa Mulungu, ndipo Yoswa anatengera Israeli kuwoloka kupita ku dziko lolonjezedwa. Zangwiro, ngati ife tingaziwone izo, momwe Mulungu anasunthira kumbuyo uko mmasikuwo. Chirichonse chimayenda bwino, iwo ankaganiza kuti iwo anali atakhazikika bwino; koma pamene nthawi ya lonjezo inayandikira, apo panadzauka Farao yemwe sankamudziwa Yosefe. Zinthu zinayamba kuyenda mosiyana, ndipo inali nthawi ya chiwombolo. Anthu anayamba kubuula ndi kulira, ndipo kenako Mulungu anatsika kuti adzawawombole iwo. Zangwiro bwanji!

18 Ndiyeno Iye anatumiza munthu, mwana anabadwa, mwana wachirendo, ndipo iye analeredwa moyo wachirendo, koma Mulungu anali ndi dzanja Lake pa iye. Mose, momwe

iye anabisidwira mmantcheza. Anabadwa mu nthawi ya chizunzo, basi monga Khristu. Anabadwa ali mwana woyenera, chimodzimodzi monga Khristu. Ndipo iye anabadwa mu dziko lino, kuti adzakhale wowombola, chimodzimodzi monga Khristu. Ndipo, oh, momwe iye, ntchito yake, momwe iye anali wopereka lamulo, anakwera pamwamba pa mapiri ndipo anakakhalapo masiku forte, anabwererako ndi Lamulo. Ndipo iye, tchimo lake lomufooketsa linali kupsyamtima, iye anaswa malamulo. Anabwereranso pamwamba, kusonyeza kuti unsembe umenewo uyenera udzafe, kudzathapo.

19 Chimodzimodzi monga Yesu anapita ku chipululu masiku forte, ndipo pamene Iye anatulukirako, Yesu, Satana anakomana naye Iye mmalo Ake ofooka, monga iye anachitira ndi Mose. Malo ofooka a Yesu anali njala. Iye anati, “Ngati iwe uli Mwana wa Mulungu, lamulira miyala iyi kuti isanduke kukhala mkate.”

20 Yesu anati, “Kwalembedwa, ‘Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha.’” Iye ankadziwa kuti iye anali asanakumane ndi Mose pamenepo. Iye ankadziwa kuti iye anakumana ndi Chinachake pambali pa Mose, pakuti Yesu ankawadziwa Mawu.

21 Ndipo pali chirichonse chimene mpingo ukuyenera kuchidziwa lero, ndi Mawu a Mulungu, momwe mungawakhazikitsire Iwo pamodzi ndi kuwayika Iwo mu mtima wanu.

22 Pakuti, ili ndi tsiku, abale, inu mudzandichitira ine umboni, tsiku la “ism.” Ine ndakhala ndikuphunzira Genesis kwa zaka ziwiri, za Genesis. Ndicho chiyambi, kupita patsogolo, mutu wa mbewu. Ndipo inu mukuzindikira kuti mipatuko yonse iyo ya tsiku lino inayambira mu Genesis. Iyo inali ndi chiyambi chake mmbuyo mu Genesis, kutsirizira kuno mu tsiku lotsiriza.

23 Mwachitsanzo, ambiri a iwo, monga momwe chipembedzo chokhazikika chija chinayambira mwa Kaini. Momwe izo zinatulukira ndi kubwera pansi kudzera mwa ana a Nowa, Hamu. Kuchokera mwa Hamu, iye anali ndi Nimrodi. Nimrodi anamanga nsanja ya Babulo. Babulo anabwera mpaka mmusi kudzadutsa mu nthawi ya Mfumu Nebukadinezara, ndipo mpaka uko mu Chivumbulutso, Babeloni. Momwe kambewu kakang’ono kaja kanayambira kumbuyo uko kumbali ya kummawa kwa zipata za Edeni, kumabwera mpaka mmusi, kudzatsirizitsa. Mitundu yonse ya mipatuko ndi chirichonse zinayambira kumbuyo uko, kudzazitsirizitsa zokha mpaka kumapeto.

24 Tsopano, izo zikutikakamiza ife kuti tizipenyetsetsa, tizikhala osamalitsa, tizikhala okhazikika mu Mawu. Zinthu zambiri zikuchitika lero zimene siziri mwamalemba. Tiyeni tiwone Lemba, tikhale otsimikiza pamene ife tikulondola. Ndizo zomwe ife takhala tikuyesetsa kuti tiphunzitse sabata ino.

25 Chinthu chachikulu kwambiri chimene ine ndachipeza motsutsa mpingo usikuuno, ndi mantha, aliyense akuchita mantha pafupi kufa ndi chinachake. Kodi inu mukuchita mantha ndi chiyani? Ngati munthu wabadwa mwatsopano, iye ayenera kukhala wokondwa, wosaderankhawa. Chimodzimodzi monga anyamata awa akuimba kuno, ndi m'bale akuchitira umboni kumbuyo uko, momasuka basi! Palibe chinthu chimene chingakuvulazeni inu. Palibe chatsopano, palibe chamtsogolo, palibe chimene chingatilekanitse ife ku chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu. Mulungu analonjeza!

26 Iye anaitana, mwa kusankha. Iye anawuyika mpingo Wake mu dongosolo. Yesu anati, "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate atamukoka iye." Inu simunabwere kwa Mulungu chifukwa chakuti mumafuna kutero; inu munabwera chifukwa Khristu anakuitanani inu. Mulungu anakuitanani inu. "Ndipo iye amene adza kwa Ine, Ine sindidzamtaya mwanjira iliyonse. Ine ndidzampatsa iye Moyo wosatha," osati kungokhala kwa sabata, chitsitsimutso chimodzi kwa chimzake; koma wosatha, Moyo Wamuyaya, "ndipo ndidzamuukitsa iye pa tsiku lotsiriza." Oh, mai! Ngati izo sizikuchotsa mphepo mu kuyenda panyanja kwa Satana, ine sindikudziwa chimene chimatero.

Mukuti, "Inu mukudziwa bwanji?"

Ine ndinati, "Yesu ananena chomwecho, PAKUTI ATERO AMBUYE."

27 Yesu ananena chomwecho, izo zikukhazikitsa izo. Ngati Iye ananena Izo, ine ndikuzikhulupirira Izo. Iye ananena, mu Yohane 5:24, phunziro lokondedwa kwa ine, "Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzabwera ku chiweruzo koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo."

Mukuti, "Ndizo zophweka kwambiri, M'bale Branham."

28 Palibe munthu, palibe munthu amene angakhoze kukhulupirira Yesu kuti angakhale Khristu, mu mtima wake, ndipo adzakhala munthu yemweyo amene iye anali poyamba. Sangakhoze kuchita izo. Ayi, bwana.

29 Monga ine ndinanena usiku wathawu. Kumwa, kusuta, juga, zinthu zonse izo si tchimo. Si tchimo kutchova juga, ayi ndithu, kapena, kutchova juga si tchimo, kani, kusuta si tchimo, kumwa si tchimo, kutukwana si tchimo, ndi chikhumbo cha tchimo! Chifukwa ndiwe wochimwa, ndi chifukwa chake iwe umachita zimenezo. Ngati iwe ukanakhala Mkhristu, iwe sibwenzi ukuchita zimenezo. Iye anati, "Iye amene akonda dziko lapansi kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri mwa iye, ngakhale mwa iye." Kotero tsopano iwe mwina ndi a . . . Inu simunayambe mwamuwonapo Mkhristu wa theka.

30 Ine ndinamufunsa winawake usiku wina, ine ndinati, "Kodi ndinu Mkhristu, m'bale?"

Anati, "Ndine Mkhristu wabwino kwambiri."

Ine ndinati, "Ayi, inu simuli."

31 Palibe Mkhristu wabwino kwambiri. Ndi angati anayamba amuwonapo munthu woledzera-wosaledzera? Palibepo. Ndi angati anayamba awonapo mbalame yoyera-yakuda? Palibepo. Ndi mwina...Inu simunayambe mwamuwonapo wochimwa-woyera. Inu mwina munabadwa kachiwiri kapena inu simunabadwepo kachiwiri. Inu mwina muli kumbali imodzi ya mpanda. Ndipo tsopano ngati mwabadwa mwatsopano, inu muli nawo Moyo wosatha, ndipo mulibe kanthu mkati mwanu...Zinthu zakale zonse zapita, ndipo pali basi—Kasupe. Madzi owawa ndi okoma sachokera pa Kasupe yemweyo. Mukuona? Mtengo umadziwika ndi chipatso chimene iwo umabala. "Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo."

32 Kalekale, anthu onse a Methodisti ankaganiza, "Mnyamata, ife tiri nawo Iwo, ife tikhoza kufuula." Atatha masiku a Luther, iwo ankaganiza chifukwa iwo anali kufuula kuti anali nawo Iwo. Ine ndimakhulupirira mu kufuula, nanenso, koma icho si chifukwa chimene ine ndiri nawo Iwo; ndicho chikhumbo kuti ine ndiri nawo Iwo.

33 Achipentekoste anadzabwera, anayankhula mmalirime, iwo anati, "Oh, tsopano ife tikudziwa ife tiri nawo Iwo." Kodi inu munatero? Zatsala pang'ono kusintha malingaliro anu tsopano. Izo si Iwo, inu mupeza kuti izo si Iwo.

34 M'bale! "Wokondedwa Mwanawankhosa wakufa, Magazi Anu ofunika sadzataya konse mphamvu Yake mpaka Mpingo wonse wowomboledwa wa Mulungu udzapulumutsidwe kuti usadzachimwenso." Mwaona, ichi ndi chimene icho chiri, "Chirichonse kuyambira mwa chikhulupiriro ine ndinawona mtsinje umene mabala Anu osefukira amapereka, chikondi chowombola chakhala chiri nkhani yanga, ndipo chidzakhala mpaka ine ndidzafe."

35 "Ngakhale ine ndingamayankhule ndi malirime a anthu ndi a Angelo, ndipo ndiribe chikondi, izo sizindipindulira ine kanthu. Ngakhale ine ndapereka chuma changa chonse kudyetsa osauka, izo sizindipindulira ine kanthu. Ngakhale ine ndiri nayo mphamvu yosuntha mapiri, ndi zina zotero, izo sizindipindulira ine kanthu. Pamene pali maulosi, iwo adzalephera. Ndipo pamene pali malirime, iwo adzaleka. Ndipo pamene pali chidziwitso, icho chidzachoka. Koma pamene chikondi changwiro chabwera mu mtima wa munthu, ziwanda zonse ku gehena sizidzakhoza konse kuzisokoneza izo." Uko nkulondola.

36 Ngati mkazi wanga akanati—akanamandilemekeza ine chifukwa iye amandiwopa ine, ine sindikanakhala...Ine ndikanamachita mantha kuti ndimusiye iye. Koma iye amandikonda ine. Iye ali nacho chidaliro mwa ine chifukwa iye

amadziwa kuti ine ndimamukonda, ndipo iye amandikonda ine. Tsopano pamene ine ndikuchokapo, ine sindimasowa kunena kuti, "Tsopano, Akazi a Branham, ine ndikusiyirani inu lamulo la dongosolo pano limene inu muyenera kumalichita, mulu wa madongosolo. Inu musadzayang'ane pa mwamuna wina aliyense, inu simudzachita *izi*, kapena inu. . .Ine. . ." Bwanji, iye basi. . .Izo zimangochitika zokha. Ine ndimamukonda iye ndipo iye amandikonda ine, ndipo izo zimangokhazikitsa izo, ine ndimangopitirira basi.

37 Umo ndi momwe zimakhalira kumukhalira moyo Khristu. Aleluya! Iwe umangomukonda Iye ndi mtima wako wonse, solo, ndi malingaliro, ndi kumapitirira nazo, ndizo zonse. Palibe choipa chingakhoze kubwerapo. Uko nkulondola. Chifukwa, muno, chinthu chonsecho, ndiwe wakufa. Iwe ndi wakufa, ndipo moyo wako wabisika mwa Mulungu, kudzera mwa Khristu, kusindikizidwa mmenemo ndi Mzimu Woyera. Mdierekezi angakupeze bwanji iweyo? Ayi.

38 Inu muitenge galimoto ya bokosi, iwo amayamba kulongeza izo, ndi kulongeza izo, pa galimotoyo. Ambiri a anthu inu pano, ine ndikudziwa ena a inu amene mumalongeza magalimoto. Ndipo iwo amazungulira, iwo amaitanitsa zochuluka chonchi *apa* ndi zochuluka chonchi *uko*. Koma galimoto imeneyo isanasindikizidwe, woyang'anira amayenera kubwerapo. Iye amadzasuzumira ndipo iye amawona kuti chirichonse chiri mmenemo, mmalo mwake, ndipo chirichonse chakonzeka. Izo zikupita kwawo. Chabwino, ngati pali chirichonse chomasuka, ndipo kuwopa kuti izo zingasweke, iye amati, "Zitulutseni izo, muzikonzenso izo kachiwiri kufikira mutakwanitsa izo." Ndipo pamene izo zamangidwa pamodzi ndi kulongezedwa ndi kuikidwa pansi, ndiye iye amadzamenyetsa zitseko ndi kuikapo chisindikizo, ndipo palibe amene angaswe chisindikizo chimenecho mpaka iyo itapita ku malo ake. Kulondola uko?

39 Umo ndi mmene zimakhalira pamene amati, Aefeso 4:30, "Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiwombolo chanu." Muli ndi nthula zina zomasuka, Mulungu adzazichotsa izo mwa inu ndi—ndi kuzikonza izo inu musanasindikizidwe kulowa mu Ufumu.

40 Mwamuna aliyense muno, ndi mkazi aliyense, wopanda ubatizo wa Mzimu Woyera; chifukwa chokhacho chimene inu mulibe Iwo, chifukwa inu simumakhulupirira. Uko nkulondola. Kukhulupirira! Ife tinazitenga izo sabata ino ndi kuzitsimikizira izo, kuti Abrahamu anakhulupirira Mulungu, mwa chikhulupiriro. Uko nkulondola.

41 Tsopano, chimenecho ndi chiphunzitso chabwino cha Baptisti, kumukhulupirira Mulungu. M'bale Tom, inu mukudziwa, ine ndikuganiza inu munachokera mu mpingo

wa Baptisti, umene iwo amati "khulupiririrani Mulungu." Chomwechonso ine ndinkatero. Ndi mpingo wabwino kutulukamo. Oh, oh, ndikhulululukireni ine, ine sindimatanthauza kuti ndinene zimenezo. Tsopano, mphindi chabe, ine ndiribe kanthu kotsutsa Abaptisti, iwo ali nawo mtolo wonse wa zinthu zabwino.

42 Koma penyani, m'bale, ine ndinawamva iwo pa wailesi, tsiku lina, munthu, mtumiki wabwino wa Baptisti, akuyesetsa kuti alambalale Machitidwe 19. Iye anati, "Apollo sankamudziwa Yesu, kotero ndi chifukwa chake iwo ankayenera kuti abatizidwenso kachiwiri." Oh, ayi!

43 Apollo ankamudziwa Yesu, ndipo iye anali kutsimikizira, mwa Mawu a Mulungu, kuti Yesu anali Khristu. Ameni. Ndipo iye anati, "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene inu munakhulupirira?" Uko nkulondola.

44 A-. . .Mulungu anamupatsa Abrahamu lonjezo, ndipo iye anakhulupirira lonjezo, ndipo ilo linawerengedwa kwa iye ngati chirungamo; koma Iye anamupatsa iye chizindikiro cha mdulidwe, ngati chisindikizo cha lonjezo. Aleluya! Iwe umakhulupirira Mulungu, mwa chikhulupiriro, kuti iwe wapulumutsidwa, ndipo umamulandira Iye; ndipo, pamene utero, Mulungu amakupatsa iwe Mzimu Woyera ngati chisindikizo cha lonjezo limene Iye anakulonjeza iwe. Mzimu Woyera ndi mphatso ya Mulungu, ndiko kulondola, umene umadula mtima, umadula mnofu wotsalira, ndikukupanga iwe kukhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu. Ameni. Chabwino, ndi zimenezotu pamenepo. Palibe chimene inu munkayenera kuchita nacho, inueni, ndi mphatso ya Mulungu. Ndipo pamene iwe ukhulupirira molondola, Mulungu amapereka Iwo kwa iwe. Ndi mwa chikhulupiriro. Iwe. . . Tsopano, chikhulupiriro si chimene Iwo uli.

45 Chimodzimodzi ngati ine ndiri ndi kotala, ndipo lofu ya buledi mtengo wake ndi kotala. Kotala. . .[M'bale Branham akuponya khobidi—Mkonzi]. Ine ndiyitola iyo pakapita kanthawi. Kotala si lofu ya buledi, koma kotala imagula lofu ya buledi. Ndi ntchito-. . .ndizo. . .Ndi yomwe imagula lofu ya buledi. (Zinapezeka kuti, izo zinapezeka kuti ndi theka la khobiri kuchokera ku Africa, kotero ine ndikuganiza ndi chifukwa chake iyo inatembenuka.) Chabwino. Kotala si lofu ya buledi; kotala imagula lofu ya buledi.

46 Chikhulupiriro ndi chimene inu muli nacho mwa Mulungu. Ndipo zimenezo, pakumuzindikira Mulungu, chifukwa cha chikhulupiriro chanu, zimakupatsani inu Mzimu Woyera umene umadula mtima ndi makutu. Ndi kulondola uko? Zimakupanga iwe kukhala cholengedwa chatsopano.

47 Tsopano, Mulungu akukonzekera kuti awombole. Ife tinapeza kuti iye anali, Mose anali akumutengera mwana wake

yemwe uko, kuti akawawombole ana a Israeli, osadulidwa. Ndipo Zipporah anatenga mwala wakuthwa, nadula khungu la mwana wake, ndipo analiponyera ilo pamaso pake, anati, "Ndiwe mwamuna wamagazi kwa ine."

48 Inu mukudziwa, kodi inu munayamba mwawerengapo izo mwatcheru chomwecho? Mose anali ndi kupsyamtima, inu mukudziwa, kumene potsiriza kunamulepheretsa iye kukalowa mdziko lolonjezedwa, kupsya mtima kwake. Ndipo Mulungu anali atamukhazika iye kumbuyo uko ndi kumupatsa iye mkazi wamng'ono-waukali, nayenso. Ine ndikuganiza iwo anali ndi vuto lina kumbuyo kwa chipululu icho, sichoncho inu? Mulungu amadziwa momwe angakuchepetsere iwe. Kotero, Iye anamukonza iye kumbuyo uko kudzera mwa mkazi wamng'onoyo, anawonetsera. Iye anadula khungu limenelo ndipo analiponyera ilo pamaso pa iye, anati, "Ndiwe mwamuna wamagazi." Mai! Iye anadziwa momwe angamukonzere iye, kuwuchotsa mkwiyo umenewo mwa iye. Chabwino.

49 Ndiye iwo anapita kumeneko, ndipo iye anachita zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa. Ndipo zindikirani! Oh, mai, ine ndinamverera Chinachake chikundikhudza ine! Taonani momwe Yambre ndi Yane, akasidi awiri amenewo, anaima pamenepo ndipo anachita zozizwitsa za mtundu womwewo zimene Mose ndi Aroni anachita, anapita nawo limodzi ndi iwo.

50 Kutsanzira! M'bale, ife tiri nalo dziko lodzaza ndi zimenezo lero. Mpingo wadzaza ndi zimenezo lero, kufanizitsa kwa chithupithupi. Ndipo pali chinthu chimodzi tsopano, kuti tizidule izi, zindikirani. Monga mphunzitsi wamkulu wa Baibulo, tsiku lina, pa wailesi, ananena, kuti, "machiritso Auzimu anali a mdierekezi," kuti, "mdierekezi amachita machiritso Auzimu." Ine ndikufuna inu mundipezere ine Lemba pamene mdierekezi anayamba wachitapo machiritso Auzimu, pamene iwo analonjezedwapo konse ndi iye.

51 Mulungu anati, "Ine ndine Ambuye," Masalmo 103:3, "Ine ndine Ambuye Yemwe ndimachiritsa matenda anu onse."

52 Ndipo Yesu anati, "Ngati Satana atulutsa Satana, ndiye kuti ufumu wake wagawanika motsutsana." Iye sangakhoze kuchita zimenezo. Iye sangakhoze kudzitulutsa yekha. Chotero machiritso onse, ziribe kanthu kumene iwo akuchokera, amabwera ndi Mulungu yekha.

53 Ndipo penyani amatsenga awa. Iwo amakhoza kubweretsa nsabwe, koma samakhoza kuzichotsa izo. Iwo samakhoza kuchiza. Iwo amakhoza kuchita chozizwitsa, koma iwo samakhoza kuchita machiritso. Machiritso amakhala mwa Mulungu, yekha. Ndipo pamene iwo anaitanitsa zithupsya, Aigupto anafala ndi zithupsya, iwoeni.

54 Ndipo iwo anati, "Ichi ndi chala cha Mulungu." Aleluya! Ine ndikuganiza za zimenezo "chala cha Mulungu." Ngati. . .

Mulungu akhoza kutsegula diso lakhungu ndi chala Chake, "ichi ndi chala cha Mulungu," akhoza kuchita zinthu zonse izi. Taonani chimene Iye anachita ndi chala Chake, Iye anachiritsa odwala ndi kuwukitsa akufa. Zinthu zonse izi Iye anazichita ndi chala Chake. Koma pamene Iye anapita kutsatira nkhosa yotayika, Iye sanagwiritse konse ntchito chala Chake, Iye anaiyika iyo pa phewa Lake ndi kuibweretsa iyo mkati. Aleluya! Ndi chitetezero chotani, nkhosa yotayika pa phewa Lake; osati chala Chake, Iye sanachigwiritse ntchito. Iye anagwiritsa ntchito phewa Lake kuti anyamulirepo nkhosa. Zindikirani.

55 Kenako Mulungu, atatha kumukonza Mose, kumukonzekeretsa iye, anatumiza zi—zizindikiro, ndiye chizindikiro chotsiriza (ife tinachitenga usiku wathawu) chinali imfa. Ndipo ife tinapeza kuti, iyo ndi mfa yauzimu mu mpingo, mliri wotsiriza tsopano, mpingo ukuuma, ukuwulukira kutali. Uko nkulondola. Ife tikukhala mu nthawi yowopysa. Momwe kuti mpingo, akale omwe kale ankakhala nacho kwenikweni chigonjetso, akutaya, nthawi yakufa, kulola Magazi achoke kutsogolo kwa chitseko. "Pamene Ine ndiwona Magazi Ine ndidzapyola pa inu."

56 Ankabwera mmwamba, kudzalowa mu Thanthwe lokanthidwa. Zindikirani pamene iwo anabwera ku Thanthwe, iwo anali nacho chosowa. Tsopano, Mose anakantha Thanthwe ndi ndodo. Apo ndi pamene ife tinalekezera usiku wathawu. Anakantha Thanthwe ndi ndodo, ndipo ndodo inali ndodo ya chiweruzo cha Mulungu. Ndipo iye anakantha Thanthwe, ndipo munali mphanga m'mbali mwa kumanzere kwa Thanthwe. Pamene ana a Israeli anamva njala, iwo ankapita kumeneko. Ndipo mng'oma wa njuchi, njuchi zinali zitalowa mmenemo ndipo anali atapanga mng'oma, ndipo iwo amatenga uchi kuchokera mu Thanthwelo. Chirichonse chimene iwo ankachisowa chinali mu Thanthwelo. Thanthwelo linkatsatira mpingo, ndipo thanthwelo linali Khristu Yesu. Pamene iwo amva ludzu, iwo ankamwa kuchokera mu Thanthwe. Pamene iwo amva njala, iwo ankadya kuchokera mu Thanthwe. Kulikonse kumene iwo ankapita, Thanthwe linkawatsatira iwo. Ndipo Thanthwe likutsatirabe mpingo! Khristu ndiye Thanthwe limene linali mu chipululu. Zindikirani tsopano, ndiye, Thanthwe lomwelo!

Nzosadabwitsa pamene iye analowa mu Yerusalemu, iwo anati, "Mpangeni iye akhale chete, apangeni iwo akhale chete."

57 Iye anati, "Ngati iwo akhale chete, miyala, miyala idzafuula nthawi yomweyo." Chinali chiyani chimenecho? Mwala Waukulu Wapangodya uja unabwera, ukugudubuzika pakati pa miyalayo. Chinachake chinkayenera kuchitika, miyala ikufuula mokweza!

58 Pamene mkazi amene anali ndi vuto la magazi kwa zaka zambiri, iye anayankhula kwa Thanthwe, ndipo Thanthwe

linatulutsa machiritso. Pamene Lazaro anali atafa, Marita anayankhula kwa Thanthwe, ndipo Ilo linabweretsa chiukitsiro. Pamene iwo anali panyanja, panachita namondwe, ndipo ngalawa yaing'ono yakale ikugwedezeka uku ndi uku ngati kuti chitsekero cha botolo chavuka pakati pa nyanja.

59 Mkazi anati kwa ine, kuno osati kale litali, iye anati, "M'bale Branham," iye anati, "Yesu sanalinso ngati munthu wamba." Anati, "Iye anali mneneri, koma inu mumayesera kumupanga iye Mulungu."

Ine nditani, "Iye anali Mulungu. Iye mwina anali Mulungu kapena wachinyengo."

Ndipo iye anati, "Oh, iye anali munthu wabwino, iye anali wambalume. Koma iye sakanakhoza kukhala Mulungu, iye sanali Waumulungu."

Ine ndinati, "Iye anali Waumulungu. Iye ankayenera kukhala Waumulungu. Ngati Iye anali munthu, Iye anabadwa kubadwa kwa kugonana; koma Iye anabadwa kubadwa kwa namwali, kotero Iye anali Magazi a Mulungu. Baibulo linati, 'Ife tinapulumutsidwa ndi Magazi a Mulungu.'"

Iye anati, "Ine nditsimikizira izo kwa inu, iye sanalinso kuposa Mulungu. . .osaposa a—a—mneneri, ndipo iye sanali Waumulungu."

Ine ndinati, "Ngati inu mungakhoze kutsimikizira izo mwa Baibulo."

Iye anati, "Ine ndichita zimenezo."

Ine ndinati, "Tiyeni timve Lemba lako."

Iye anati, "Mu Yohane Woyera, mutu wa 11, pamene Yesu anapita kumusi tsiku limenelo ku manda a Lazaro."

Ine ndinati, "Ine ndikukumbukira zimenezo."

Anati, "Iye analira. Baibulo linati, 'iye analira.'"

Ine ndinati, "Izo nzoona." Ine ndinati, "Kodi izo ziri ndi chochita chanji ndi zimenezo?"

Iye anati, "Izo zikutsimikizira kuti iye sanali Waumulungu, chifukwa iye sakanakhoza kulira ndi kukhala Waumulungu."

60 Ine ndinati, "Penyani, mkazi. Iye anali Mulungu-Munthu." Ine ndinati, "Pamene Iye anapita kumusi uko, akulira, pamene Iye anali kulira, Iye anali Munthu. Koma ine ndikukuuzani inu, pamene Iye anakokera chimango chaching'ono icho pamwamba apo, ndipo nkudzati 'Ine ndine Chiukitsiro ndi Moyo'! Ndipo Iye anayankhula kwa munthu yemwe anali atafa masiku foro, thupi lake linali litavunda, mphutsi za khungu zinali kukwawa mkati ndi kunja. Chivundi chinamudziwa Mbuye wake! Ndipo munthu, amene anali atafa kwa masiku foro, anaima pa mapazi ake ndipo anakhalanso moyo. Ameneyo anali woposa munthu akuyankhula. Ameneyo anali Mulungu." Inde, bwana.

61 Iye anali Munthu pamene Iye anali pamwamba apo pa phiri usiku umenewo, anadzatsika pansi, anayang'ana ponse pozungulira pa mtengo, kuti apeze chinachake choti adye, mtengo wa mkuyu, kuyesera kutero. Iye anali ndi njala. Iye anali ndi njala pamene Iye anali Munthu. Pamene Iye anali kuyang'ana pa mtengo umenewo, Iye anali Munthu. Koma pamene Iye anatenga mabisiketi faivi ndi zidutswa ziwiri za nsomba, ndi kudyetsa faivi sauzande, ameneyo anali woposa Mulungu. . . woposa munthu, ameneyo anali Mulungu mwa Munthu ameneyo. Inde, bwana.

62 Zoonadi Iye anali Munthu pamene Iye anali atagona mu ngalawa imeneyo, ndipo choimitsiracho chinali ngati chotsekera botolo; anati, "Oh, ine ndipita ndikamukankhe iye mozungulira, ndikumunjanjitsa iye mmwamba ndi pansi," ziwanda teni sauzande za m'nyanja zinalumbira kuti zimumiza Iye usiku umenewo. Iye anali Munthu, wotopa kwambiri mwakuti Iye sankakhoza kusuntha. Koma pamene Iye anayika phazi Lake pa chingwe cha ngalawa imeneyo, ndipo nkudzati, "Mtendere! Pakhale bata," ndipo mphepo ndi mafunde zinamumvera Iye, ameneyo anali woposa Munthu. Ameneyo anali Mulungu. Inde, bwana.

63 Pamene Iye anafa pa Kalvare, Iye anafuula kufuna chifundo ngati munthu. Iye anali Munthu, pamene Iye ankafa. Koma pamene Iye anawuka, mmawa wa Isitara, Iye anatsimikizira kuti Iye anali Mulungu. Ndiko kulondola, anauka kwa akufa!

64 Nzosadabwitsa wolemba ndakatuloyo anati, "Kukhala moyo, Iye anandikonda ine; pakufa, Iye anandipulumutsa ine; kuikidwa mmanda, Iye ananyamulira machimo anga kutali; powuka, Iye anandilungamitsa kwaulere kwanthawizonse; tsiku lina Iye akubwera, Oh, tsiku laulemelero!"

65 Mulungu-Munthu! Mulungu anali mwa Mwana Wake, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini. Iwo anali atamunenera Iye kukhala a—a "wamatsenga," ndi a—a "wambwebwe," ndi "mdierekzi," ndi "Belezebule," ndi chirichonse. Koma Iye anali Mulungu, Emanuele, akukhala pakati pathu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini. Ife tinali nazo izo pa funso mmawa, mulimonse, ife tidzafika pa zimenezo ndi kudzamalizitsa izo mawa. Chabwino.

66 Akubwera pamwamba, Thanthwe lokanthidwa lija. Pamene iwo asowa chirichonse, iwo ankapita ku Thanthwelo. Tsopano, pambuyo pa zonsezo, ndi madalitso ndi zinthu, iwo ankang'ung'udzabe.

67 Iwo anafika ku malo otchedwa Kadesi-barnea. Tsopano ife tikufuna kuti tiphunzire izi kwa mphindi yokha. Kadesi-barnea anali mpando wachiweruzo wa mdziko, mu tsikulo. Izo zikupezeka, mutu wa 13 tsopano, wa Numeri. Ndipo mupite kumakalemba Malemba, ngati inu mukufuna, tsopano.

M'menemo munali mpando wachiweruzo. Mukawerenge mitu ya m'mbuyo kwa iwo, mu kwanu—mu kuphunzira kwanu. Ife tikungoyenera kugunda malo okwerawo tsopano, mu chitsitsimutso cha masiku atatu kapena foro monga chonchi. Sitingakhoze kuphunzira izo ndime ndi ndime. Koma iwo unali mpando wachiweruzo. Panali chitsime chachikulu pamenepo. Anali ndi zitsime zazing'ono zambiri kuchokera pa icho, timitsinje kapena—kapena akasupe amachokera ku kasupe wamkulu uyu, Kadesi-barnea.

68 Choyimira changwiro cha mpingo. Mpingo ndi mpando wachiweruzo. Chiweruzo chimayambira mnyumba ya Mulungu.

69 Kumeneko Israeli anasonkhana mozungulira, ku Kadeshi. Ndipo tsopano Mose ananena apa, ndime ya 1, mutu wa 13.

> *Ndipo* Ambuye *anayankhula kwa Mose, anati,*
>
> *Utumize iwe amuna, kuti iwo akathe kufufuza dziko la Kanani, limene Ine* ndalipereka *kwa ana a Israeli: kuchokera ku fuko lirilonse la makolo awo iwe udzatumizako mwamuna mmodzi, mmodzi aliyense wolamulira mwa iwo.*

70 Tsopano, Mulungu anakonza kuti iwo atumize amuna thwelovu, mmodzi kuchokera ku fuko lirilonse, kuwatumiza iwo ku dziko la Kanani, kuti akazonde dzikolo, kuti akawone ngati iwo anali malo abwino kapena ayi. Azondiwo anapita, mmodzi kuchokera ku fuko lirilonse. Mmodzi kuchokera mwa Dani, Aseri, kudutsa konseko, mpaka iwo anapeza amuna thwelovu.

71 Changwiro cha mpingo lero, mmaulendo athu. Ife tikupita chokwera, mpaka, ine ndikukhulupirira kuti mpingo waima lero ku Kadesh-barnea, chiweruzo! Tsopano, Mulungu andithandize ine. Ine ndikudalira kuti Mulungu andithandiza ine kuti ndipeze izi, izo zidzama bwino komanso mwakuya.

72 Kutumiza zazikulu. Kumbukirani, iwo anali atafika mpaka apa chifukwa Mulungu anali atawalonjeza iwo. Ndipo mu ulendo wonsewo, iwo anali nazo zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa, ndipo tsopano iwo afika mpaka komwe kumalire.

73 Ndipo ine ndikukhulupirira ife tiri pa malire usikuuno. Ine ndinali kudabwa za misonkhano yanga yonse ndi zinthu, momwe ine ndimayenera kuzilepheretsa izo. Ine ndikukhulupirira moona, Mpingo usanakhale ndi Mkwatulo, iwo uyenera kudzakhala nacho chikhulupiriro chokwatulitsa. Ife tikulephera nkomwe kukhala nacho chikhulupiriro cha machiritso Auzimu, ndiye munene za chikhulupiriro chokwatulitsa. Tiyenera kudzakhala nacho chikhulupiriro chimene chiti chidzasinthe ndi kulifulumizitsa thupi ili, ndi kudzatengedwera kutali. Ine ndikukhulupirira kuti pali Mpingo uli paulendo wake usikuuno, mphamvu ya Mulungu wamoyo, kuti anthu azidzayankhula Mawu *apa* ndi *apo*, ndipo izo zizidzawala ngati mphezi. Ndipo Mpingo ukutuluka; osati wowerenga maganizo, osati

zina izi zochita kuvala, zodzipangitsa-kukhulupirira; koma weniweni, woona, weniweni, wodzozedwa, Mzimu Woyera, Mpingo woyitanidwa-atuluke! Ameni.

74 Apa iwo ali, atayima pa Kadesi-barnea. Iwo anati, "Pitani kumeneko. Dzikolo linapatsidwa kwa ife zaka mahandiredi ambiri apitawo, ndi Mulungu, kudzera mwa atate athu. Ife ndife Mbewu ya Abrahamu. Mulungu watitsogolera ife motetezeka mamailosi forte ena osamvetsetseka awa kuchokera ku Igupto, mpaka ku dziko la mmalire pa Kadeshi." Iwo anali atafika kumeneko mmasiku pang'ono, koma, kumbukirani, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo, zinawapangitsa iwo kuyendayenda kwa zaka forte.

75 Kusakhulupirira! Zindikirani, mpingo umene ine ndikuwukambawu, kuyankhula mophiphiritsa. Chimene Chakale chinali, Chatsopano chiri, mwanjira yokulirapo. Chimene chachibadwa chinali, chauzimu chiri.

76 Tsopano, Kadeshi. Ndipo pamenepo iye anati, "Tsopano inu tulukani, ndipo mukazonde." Mulungu anawatumiza iwo; Mose sanatero. Mulungu anawatumiza iwo kumeneko, ndipo anati, "Mupite kumeneko ndipo mukazonde dzikolo, ndipo mudzabwerere ndi kudzatiuza ife ngati ilo liri dziko labwino kapena loyipa, kapena ngati ife tingakhoze kukalitenga ilo, kapena chiyani *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*. Inu mupiteko ndipo mukafufuze."

77 Ndipo thwelovu anapita uko. Iwo anadula mulu wawukulu wa mphesa. Inu mukudziwa za hule Rahabu, ndi zina zotero. Chabwino. Iwo anapita ndipo anakadula mulu uwu waukulu wa mphesa, ndipo anabwererako. Koma mvetserani ku lipotilo, amuna thwelovu!

78 Ndipo teni kuchokera mwa thwelovuwo anati, "Oh, iwo ndi anthu owopsya." Yang'anani apa, ndi otani a—ndi mawonekedwe otani! Mvetserani kwa izi. Pamene ife tikutembenuzira tsopano ku ndime ya 17, kapena ndime ya 27, kani, kuti tiwerenge. Anapitirira ndi kukanena kumeneko amuna amene anatumidwawo. Ndipo pamene iwo anabwererako mitima yawo inakomoka, iwo anati: "Oh, iwo ndi amuna aakulu!" Mvetserani apa.

> *Ndipo iwo anawauza* iwo, *ndipo anati, Ife* tinapita kukalowa *mdziko limene* munatitumizako *ife, ndipo ndithudi ilo* likuyenda *ndi mkaka ndi uchi; ndipo* ilo liri *chipatso*. . . *chipatso cha ilo*. (Monga momwe Mulungu analonjezera. Tsopano zindikirani.)
>
> *Komabe anthuwo* ndi *amphamvu* ndipo *amakhala mdzikomo,* ndipo *amakhala mdzikomo, ndi midzi ndi yamalinga, ndi yaikuru kwambiri:*. . .*komanso ife tinawona*. . .*ana a Anaki kumeneko.*

> Ndipo *Aamaleki amakhala mdzikomo*. . .*ndi Ahiti,*. . .*Ayebusi, ndi Aamori, amakhala kumapiri: ndipo Akanani amakhala* pa *nyanja nyanja,* kapena, *gombe la Yordano.*
>
> *Ndipo Kalebu,* (aleluya), *Kalebu anawatontholetsa anthuwo pamaso pa Mose, ndipo anati, Tiyeni ife tipite uko mwakamodzi, ndipo tikalitenge ilo; pakuti ife tiri okhoza bwino kulilaka ilo.*

79 Ah, ine ndikuzikonda zimenezo! Mai! Patsogolo pang'ono chabe.

> *Koma amuna amene anakwera uko ndi iye anati, Ife sitingakhoze kupitako*. . .*kukalimbana nawo anthuwo; pakuti iwo ndi amphamvu kuposa ife.*
>
> *Ndipo iwo anabweretsapo umboni woipa wa dziko limene iwo anali atalifufuza* kufufuzira *ana a Israeli, kuti, Dzikolo,*. . .*limene ife tinapitako kuti tikalizonde, ndi dziko limene ladya okhalamo mmenemo; ndipo anthu onse amene ife tinawawona mmenemo ndi amuna*. . .*usinkhu waukulu.*

80 Mvetserani kwa zimenezo! Ndipo izo zikupitirira kunena, kuti, "Ife tikuwoneka ngati ziwala, kumbali ya iwowo." Ndiro lipoti lake.

81 Koma Kalebu ndi Yoswa anati, "Ife tikhoza kulitenga ilo! Ife tiri okhoza kukachita zimenezo." Ndi chifukwa chiyani iwo ali okhoza kukachita zimenezo? Mulungu anali atawalonjeza iwo kuti adzachita izo. Ine ndimakonda kulimba mtima kumeneko.

82 Teni a iwo. Tsopano mpingo unabwera. Ndipo iwo wafika tsopano pa malo pamene ife tafikapo titadutsa mu M'badwo wa Luther, M'badwo wa Methodisti, ndi M'badwo wa Chipentekoste, ndi kumapitirira kukafika ku malowo. Ndipo tsopano ena a anthu a Uthenga wathunthu anatembenuka mwamphamvu kutsutsa machiritso Auzimu, kumakhulupirira kuti sizinali nkomwe mu chitetezero. Chabwino, izo zinafika pa malo, abwenzi, pamene inu. . .Izo zikuyamba kuyipa kunja kuno. "Chipembedzo cha nthawi-yakale," iwo amati, "ndi chinachake chimene chinadutsa kalekale, sichingakhale nacho icho, zachulukitsa kwambiri. Ife tikukhala mu tsiku lamakono, ife tiyenera kupeza malingaliro amakono. Ife tiyenera kumakhala ndi masewero mu tchalitchi, masewero a ping-pong, ndi chirichonse, kuti tiziwagwira achinyamata athu."

83 M'bale kapena Mlongo, ngati izo zidzafike pa nthawi yoti ine ndizidzakhala ndi phwando la makadi mu tchalitchi, kuti ndiwagwire omvetsera, ine ndidzasiya kulalikira Uthenga, chifukwa Iwo wataya mphamvu Yake. Ine ndikukuuzani inu, m'bale, chimene ife tikusowa lero ndi Uthenga-wakachitidwe kachikale, wophweka, mphamvu ya Mzimu Woyera ikulalikidwa

mu kuphweka Kwake. "Amuna...Ngati Ine ndidzakwezedwa kuchokera pa dziko lapansi, Ine ndidzakokera anthu onse kwa Ine." Inde, bwana.

84 Ife lero, iwo amati, "Oh, ife sitingakhoze kubwerera mmbuyo ndi kukachita zinthu izo zimene atumwi ankachita."

85 Ife tikukhala mmasiku otsiriza, pamene Mulungu analonjeza kuti Iye adzatsanulira Mzimu Wake pa mnofu wonse. Aleluya! Ife tiri pano kumapeto kwa ulendo. Tikuthokoza Mulungu chifukwa cha Kalebu ndi Yoswa ena omwe ali okonzeka kuti awoloke, aleluya, kupita uko ndi kukabweretsako umboni, aleluya, ndi dziko lopambana! Kubweretsanso mitolo iwiri ya mphesa, ndipo iwo anali akuyenda *chonchi* kuti ayesere kunyamula izo. Ndi maziko otani! Malo otani! Tikuthokoza Mulungu chifukwa cha anthu amene awoloka, achokako ku zofunda zawo zakale, zomangidwa-unyolo, mpingo wopanda umulungu, chikhalidwe chokhuthala. Aleluya! Anafika pamalo amene iwo anawolokera mdziko la Kanani, ndipo anakadya mphesa zambiri zabwino zomwe zimakupangitsa iwe mpaka kumawukha dovu paguwa. Aleluya! Zina mwa zabwino zakachitidwe-kachikale zimenezo...Ataledzera ndi vinyo, monga Petro anamwa pa Tsiku la Pentekoste, pamene mphamvu ya Mulungu inawulanda mpingo. Aleluya! Kadesi-barnea. Ife tikhoza kuchita zimenezo!

86 Munthuyo anati, "Kodi inu mukutanthauza kundiuza ine kuti ife tikhoza kulandira Mzimu Woyera monga iwo anachitira kalekale?"

"Inde, bwana."

"Tsopano, inu mukudziwa bwanji?"

Ine ndinati, "Ine ndiri nawo Iwo! Aleluya! Umo ndi momwe ine ndikudziwira izo."

87 Ife tinali nacho choimira chokongola usiku wathawu, pamene ana a Israeli anawoloka dzikolo, anawoloka mpaka mu—mwendamnjira, chimene chinali choyimira changwiro cha ulendo wathu. Ife tinabwera kuchokera ku Kanani. Ine ndinazula chikhomo changa, mahema, ndipo ndinanyamuka (inu munatero?), kusiya magariki akale ndi miphika yophikira nyama kumusi uko, ndi kununkha kwa dziko. Anazula hema, ananyamuka, anawoloka Yordano! Aleluya! Nyanja yofiira ya Magazi a Yesu Khristu inamiza ndudu yakale iliyonse, utsi wa fodya, ndi nyansi za mdziko zinamizidwa, monga ogwiritsa ntchito aja kumbuyo uko, ndipo iwo akuyandama mnyanja. Aleluya! Nzosadabwitsa ife timafuula ndi kuvina!

88 Taonani zimene Mose anachita, anakweza dzanja lake ndipo anayimba mu Mzimu. Ndipo Miriamu anatenga nkhotcho ndipo anayamba kuvina, ndi kulumpha chokwera ndi chotsika, ndipo anatamanda Mulungu. Ndipo ana akazi a Israeli anamtsatira iye, akuvina, ndi kutamanda Mulungu, ndi kufuula. Aleluya!

Iwo anawoloka nyanja. Ogwiritsa ntchito akale onse anali atabwerera, atafa, uko mnyanja. Iwo anayang'ana mmbuyo ndipo anati, "Mnyamata, iwe sudzandivutitsanso ine." Oh, mai! Anawotcha milatho konsekonse, kukonzekera kuti azipita tsopano, ulendo wopitirira.

Tsopano iwo anati, "Kodi ife tingakalitenge ilo?"

"Ndithudi, ife tikhoza kukalitenga ilo."

"Chifukwa chiyani?"

"Mulungu ananena chomwecho!" Ndipo kumbukirani, iwo anali . . . Mulungu analonjeza kuti adzawapatsa zosowa zawo. Ife tinali nazo izo usiku wathawu.

"Iwo adzapereka chotani izo?"

"Ine sindikudziwa."

"Chabwino, mwinamwake iwo adzatumiza chitumbuwa china kuchokera kwinakwake ku a . . . "

"Munalibe kanthu kanatsalira mu Igupto, chitumbuwacho chikachokera kuti?"

"Oh, mai! Iyo si ntchito yanga."

89 Winawake ananena kwa ine nthawi ina, anati, "Kodi inu mumakhulupirira za Eliya ameneyo, nkhani ya mbalame ija kuntunda uko?"

Ine ndinati, "Ndithudi."

Anati, "Inu mukutanthauza kundiuza ine kuti mumakhulupirira mlaliki uja anakhala pansi mmphepete mwa mtsinje wa Keriti kumtunda uko, ndipo akhwangwala ankamudyetsa iye?"

Ine ndinati, "Ndithudi."

"Inu mukudziwa bwanji kuti iwo ankamudyetsa iye?"

Ine ndinati, "Baibulo linanena chomwecho." Uko nkulondola.

Anati, "Ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake, mlaliki." Anati, "Kodi ndi kuti mdziko kumene inu mukuganiza kuti akhwangwala amenewo ankapeza masangweji amenewo?"

Ine ndinati, "Ine sindikudziwa. Iwo ankawabweretsa iwo, Eliya ankawadya iwo. Ndizo zonse zimene ine ndikudziwa."

Iye anati, "Ine ndikukhulupirira inu nonse mumatengeka."

Ine ndinati, "Ayi. Ine sindingakhoze kukuuzani inu kumene Iwo ankachokera, koma Iwo ankachokera kwinakwake. Mulungu ankawabweretsa Iwo, ife timawadya Iwo. Aleluya, ndipo Iwo amabweretsa chimwemwe!"

90 Momwe izo zimachitikira, ine sindikudziwa. Mulungu amangowatumiza Iwo, ndipo ine ndimawatenga Iwo. Ine ndangolandira kumene odzaza dzanja maminiti pang'ono

apitawo, ndipo ndinawameza Iwo, akungondigirigishabe ine pamene Iwo akutsikira pansi. Ndizo zabwino! Musati mutengeke; ine sindine wopenga. Ine ndatchedwa chomwecho, koma ine sindiri. Ngati ine ndiri, mungondisiya ine ndekha, ndine wokondwa. Chabwino. Inde, bwana, ine ndikumverera mwachipembedzo kwenikweni tsopano. Oh, zedi ndikutero! Chabwino.

91 Tamuyang'anani iye. Ndi uyu apa, "Kodi ife tichita motani izo?" Tsopano, Mulungu ankavumbitsa mana pansi kuchokera kumwamba, ndipo ankawadyetsa iwo. Sichoncho Iye? Iye ndithudi ankatero. Ndipo iwo ankawatola iwo. Ife tinadutsa mu zimenezo.

92 Tsopano, icho chinali choyimira changwiro cha kudya kwathu lero. Mana amenewo sankasiya konse, iwo ankagwa usiku uliwonse, usiku uliwonse, nthawi yonse yomwe iwo anali mu ulendo wawo, kuchokera ku Igupto kupita ku dziko lolonjezedwa. Ndipo Mzimu Woyera unagwa mwamsanga pamene ophunzira anachoka ku Igupto, pa Tsiku la Pentekoste, Mzimu Woyera unabwera kuchokera Kumwamba, malo omwewo komwe manna amachokerako, ngati mphepo ya mkokomo wamphamvu, inadzadza nyumba yonse momwe iwo anali atakhala, malirime ogawanika anadzakhala pa iwo, ngati moto. Iwo anatuluka kuchokera mmenemo, akukuwa, ndi kumachita ngati anthu oledzera, akuvina, akuzandima, akukuwa, akuwukha dovu, ndi china chirichonse.

Kodi inu munayamba mwamuwonapo woledzera wachikulire akubwera kunyumba? Mnyamata, iye amatenga mbali zonsezonse za msewu, "Moni, mlendo!" Palibe chomwe chikumuvutitsa iye.

93 "Ndipo palibe kutsutsika kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene samayenda monga mwa thupi koma mwa Mzimu," Aroma 8:1. Apa iwo akubwera, akubwera Kunyumba, tsopano akuzandima pansi pa mphamvu ya Mzimu Woyera, amene anali Manna a Mulungu akutsikira pansi kuchokera Kumwamba, ndipo Iwo akhala akugwa kuyambira tsiku limenelo mpaka lero. Aliyense. . .

Inu mukudziwa chiyani? Omeri amakhala wodzaza, kuti wansembe aliyense akalowamo, amakhoza kukadya odzaza mkamwa manna apachiyambi.

94 Kodi manna amenewa amakhala nthawi yaitali bwanji? Kubwereza zomwe Izo zinali usiku watha, mu phunziro, Petro anati, "Lapani, mmodzi aliyense wa inu, mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera, pakuti lonjezano liri kwa inu, kwa ana anu, kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana." Mzimu Woyera

ndiwo basi Mzimu Woyera womwewo usikuuno monga Iwo unali kumbuyo uko pachiyambi. Kodi tingakalitenge ilo? Inde, bwana.

95 Mpingo ukufika pa Kadeshi. Kodi inu muchita chiyani? Ndi ife apa. Iwo akuti . . . Tsopano, munthu aliyense payekha, mmodzi aliyense wa inu muli pa Kadeshi, ife tinafika pamenepo.

96 Ndipo inu mukuti, "Tsopano, ngati ine—ngati ndipita kumeneko ndi kukatenga zina za chipembedzo choyera chodzigudubuza icho chimene iwo amachikamba, amayi anga andithamangitsa ine kunyumba."

97 Ndi zimenezotu pamenepo, pa Kadeshi. Kodi inu mungathe kuchita zimenezo? Inde, Mulungu analonjeza izo kwa inu. "Ine sindinabwere kuti ndidzabweretse mtendere, koma lupanga. Ine ndinabwera kudzalekanitsa abambo ndi amayi, mwamuna, mkazi, mlongo, m'bale, ndi chirichonse. Ndipo iye amene sadzasiya ake omwe ndi kunditsatira Ine, sali woyenera kutchedwa Anga. Ndipo iye amene ayika dzanja lake pa khasu ndipo nkutembenuka kuti ayang'ane mmbuyo, sali woyenera." Ndiko kulondola.

98 M'bale, ine ndikukuuzani inu, izo zikutanthauza mochuluka kwambiri kuposa kuthamanga chokwera ndi kugwirana chanza ndi mlaliki, ndi madontho pang'ono a madzi kukonkhedwera pa inu. Uko nkulondola. M'bale, izo zimayenda mochuluka kwambiri kuposa kuyenda kupita ku guwa ndi kumadya mgonero, ndi kumayenda chammbuyo ndi kukakhala pansi pa mpando wako. Izo zimatanthauza kudzigulitsa, kufa, m'bale, ndi kutenga kachitidwe-kachikale, kakutchire, chipembedzo cha mmwamba mwa buluu, chakupha-tchimo chimene sichiti . . . sichikusambitsa ndi zoyera, koma osakuphimba iwe, koma chimakuyeretsa iwe kukhala woyera, aleluya, kukuyeretsa iwe, kukuwotcha iwe, kukukwecha iwe, kukutenthetsa iwe ndi kukupanga iwe kukhala munthu watsopano. Ameni! Ndiwo mtundu wa olalikira achimidzi achikale achifundo, m'bale, koma, ine ndikukuuzani inu, Iwo udzamamatira ku nthiti zanu. Pezani wina wa Iwo. Ndiko kulondola, Iwo udzakugwirizitsani inu kudutsa mmayesero. Ameni! Ine ndikumverera ngati ndifuule, pafupifupi kwambiri. Ndicho chachikulu kwambiri . . . Inde, bwana.

99 Pamene ine ndiganiza za zimenezo, m'bale, izo ndi zotetezedwa. Mulungu ananena chomwecho. Kodi ife tingakalitenge ilo? Zedi, ife tikhoza kukalitenga ilo. "Mmasiku otsiriza Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga, ndipo Ine ndidzasonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa." Aleluya! Iye anati Iye akanadzachita izo. Mulungu analonjeza zimenezo. Ife tiri pa Kadeshi, tiyeni tipite tikalitenge ilo! Winawake anapitako uko ndipo wabweretsako mphesa zina. Ine ndikudziwa dzikolo ndi labwino. Uko nkulondola. Tiyeni tipite uko ndipo tikatenge zina za izo. Uko nkulondola.

100 Mpingo unayamba kung'ung'udza ndi kunjenjemera, ndi chirichonse. Mulungu akanautumiza mpingo kumeneko, zaka zapitazo, ngati iwo akanangomvetsera kwa Iye. Koma iwo anayamba kutsutsana ndi kukangana, ndi kumang'ung'udza pamenepo.

101 Amethodisti anali ndi chitsitsimutso chakachitidwe-kachikale mmbuyo mmasiku a Spurgeon, iwo anayamba kulandira mphatso, ndi zina zotero. Ndipo mpingo unalowa mmenemo ndi kuyamba kung'amba chinthu chimenecho, ndipo mpingo wakhala ukuyendayenda mu chipululu chiyambireni, kumangoyendayenda ukuzungulira. Iwo unagawanikana kukhala Nazarene, Pilgrim Holiness, ndi *ichi*, *icho*, ndi *ichi* ndi *icho*, ndi *icho* ndi *chinacho*, ndi china chirichonsecho, mpaka pano zakhala ngati gulu lalikulu la ine-si-ndikudziwa-chiyani. Ndi nzoona. Iwo anapanga masukulu aakulu, ndipo ankaganiza kuti iwo aziphunzitsa zafioloje za mmalo ena.

102 Monga ine ndinanenera usiku wathawu, izo zimandiyika ine m'malingaliro a malo osungiramo maliro. Kupita kumeneko, ndipo kozizira kwambiri! Iwe ukalowamo, chopimira kutentha kwa thupi chauzimu—chopimira kutentha kwa thupi chikuti "handiredi pansi pa ziro."

103 Winawake, nthawi ina osati kale litali, mkazi wachikulire wamng'ono anabwera kuchokera kumudzi, iye anadzalowa mkati, iye anali atavala diresi lake lachikale lalitali, ilo lonse lozungulira pakhosi pake pamwamba *apa*. Iye anadzalowa mkati, ndipo wake—mwana wake anamutengera iye ku tchalitchi. Iye anachita manyazi ndi iye. Iye anayenda kupita pakhomo, iye anati, "Mmawa wabwino, eledara." Analowa monga choncho.

104 Ndipo mwamuna wake, kapena, azibale ake, kapena, mwana wake anati, "Oh, Amayi! Amayi, inu mukhale chete." Iye anali atapita, anali wa mpingo wina waukulu wolemekezeka, inu mukudziwa.

105 Iye anati, "Chabwino, ulemelero kwa Mulungu! Kodi ine sindiri mnyumba ya Mulungu?" Iye sanadziwe kusiyanitsa kwake.

106 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu, m'bale, dzina lake mwina silinali mu *Ndani ndi Ndani,* monga ochuluka a iwo ali nawo, ndipo iwo amati ali nawo foro handiredi okhazikika. Koma dzina lake linalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ine kulibwino ndikhale nalo langa Kumeneko kuposa onse a *Ndani ndi Ndani*. Aleluya! Izo zimanena uyu ndi ndani: dzina linalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.

107 Iye analowa mkati ndipo anadzakhala pansi monga choncho. Mlalikiyo anayamba kunena, "Tsopano, Ambuye Yesu Khristu anabwera pa dziko lapansi kudzapulumutsa wochimwa."

108 Iye anati, “Ameni! Ulemelero kwa Mulungu! Izo nzoona, m’bale.” Ndipo aliyense anagwedeza khosi lawo nkudzatembenuka, ngati tsekwe kwinakwake, akuyang’ana pozungulira, ndikumadabwa.

109 Ndipo chotero iye anati, “Uh-um, uh-um.” Iye anali kuwerenga zolemba zake, inu mukudziwa. Chotero iye anakhala ngati anasokonezeka pamenepo, ndipo iye anati, “Uh-um, uh-um. Mundikhulululukire ine.” Anati, “Ndipo, monga ndimanenera, Ambuye Yesu Khristu anabwera ku dziko lapansi.”

Iye anati, “Ulemelero kwa Mulungu! Ndiko kulondola, m’bale. Aleluya!”

110 Kotero wothandizirayo anabwerera mmbuyo ndipo anadzamugogoda iye pa phewa, anati, “Abiti, inu mukuyenera mukhale chete kapena ife tikakuikani inu panja.” Oh, mai! Aleluya!

111 Ndicho chimene ife talowamo, ndiko kulondola, masukulu a aneneri. Ife timawalera aphunzitsi, ife timabairamo madzi akale owumitsira mitembo mwa iwo kuti tiziwasunga iwo. Iwo afa, mulimonse. Ndiyeno timaikamo madzi owumitsa mitembo kuti iwo afe kwenikweni, zina za fioloje yakale iyi yomwe iwo amaphunzitsa, “Kuti masiku a zozizwitsa anatha, palibe chinthu chotero monga chipembedzo chogwira mtima.”

112 Zikundikumbutsa ine za bambo wachikuda uko kummwera, munthu wachikulireyo ankanyamula Baibulo lake akamayenda. Anati, “Chifukwa chiyani inu mumanyamula Baibulo limenelo, mnyamata?”

Iye anati, “Ine ndimalikhulupirira Ilo.”

Anati, “Iwe sungakhoze kuwerenga liwu mwa Ilo.”

Anati, “Ine ndimalikhulupirira Ilo, mulimonse.” Anati, “Ine ndimalikhulupirira Ilo kuchokera ‘chikutiro’ mpaka ‘chikutiro,’ ndimakhulupirira ‘chikutiro’ aponso.”

Anati, “Iwe umadziwa bwanji?”

Anati, “Ilo liri ndi ‘Baibulo Lopatulika’ zitalembedwa pa Ilo.” Inde, bwana. Iye amalikhulupirira Ilo, mulimonse, sizinapange kusiyana kulikonse.

Anati, “Kodi inu mungachite chiyani,” anati, “mungachite chirichonse chomwe chiri mu Baibulo limenelo?”

Anati, “Ambuye atandiuza ine kuti ndichite chirichonse, ine ndingachichite icho.”

Iye anati, “Bwanji ngati Iye atakuuzani inu kuti mudumphe kudutsa khoma limenelo?”

Iye anati, “Ine ndingalumphe.”

Anati, “Inu mukuganiza kuti inu mungadutse kupyola khoma limenelo popanda bowo pamenepo?”

113 Anati, "Ngati Ambuye atandiuza ine kuti ndidumphe, Iye angandipangire ine bowo pamenepo." Uko nkulondola, aponso, m'bale. Aleluya! Ndicho choonadi. Mulungu atakuuzani inu kuti mudumphe, Iye adzakhala ali ndi bowo pamenepo pamene muzikafika pamenepo. Musati mudandaule nazo zimenezo.

114 Sukulu ya fioloje! Oh, mai! Inu mukudziwa zimene iwo achita? Mmalo mwake, mwa chipinda chapamwamba, iwo analoweza mmalo ndi chipinda cha nkhomaliro, anaphika tambala wina wokalamba ndipo anakonza mbale yawo ya fifite-senti, kuti aziyesera kumulipira mlaliki. M'bale, ngati munapereka chachikhumi chanu ndi kuchita zomwe Mulungu ananena kuti inu muzichita, inu sibwenzi mukukhala ndi maphwando akale a msuzi awa ndi zinthu monga izo. Ameni. (Ngakhale mafuta odzozera analumpha, pa zimenezo.) Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, m'bale, Mulungu akufuna mpingo umene ukuyenda mu chifuniro Chauzimu cha Mulungu, zokhazikika pa PAKUTI ATERO AMBUYE. Inde, bwana. Iwo achotsa kudikirira konse mu chipinda chapamwamba, monga choncho. Zomwe iwo awuchitira Mzimu Woyera, iwo aloweza mmalo mwake fioloje mmalo mwa Iwo. Winawake anatuluka ndipo akuti, "Chabwino, ife timakhulupirira *izi* ndipo ife timakhulupirira *izo*." Ndi chifukwa chiyani inu mumakhulupirira zimenezo? Izo mulibemo mu Baibulo, palibe kanthu za izo.

115 Winawake anati, "Kodi inu mukuganiza chiyani za wansembe uja kumusi kuno tsiku lina, anathawa ndi mkazi uja ndipo anamukwatira iye?"

Ine ndinati, "Iye anali nawo ufulu wotero. Iye ali nawo ufulu wochuluka woti akwatire monga ine ndachitira, kapena wina aliyense. Inu simungazipeze zimenezo mu Baibulo."

Mnyamata wina wa Chikatolika anati, "Ndi zoona zimenezo, Billy?"

Ine ndinati, "Ndi choonadi."

Iye anati, "Ziwonetseni izo kwa ine."

116 Ndipo ine ndinati, "Chabwino, ine ndizisonyeza izo kwa inu mu Baibulo, kuti 'ukwati ndi wolemekezeka kwa onse.' Aleluya! Paulo anati, 'Mwamuna aliyense azikhala ndi mkazi wakewake.' Uko ndi ndendende kulondola." Ine ndinati, "Chimenecho—chikondi cha Chiroma, ndipo palibe choonadi chinanso kwa icho kuposa maenje opanda malire a gehena." Aleluya! Ine ndimakhulupirira Mawu a Mulungu. Ine ndiyenera kukhulupirira chinachake, ndipo Ichi ndi PAKUTI ATERO AMBUYE!

117 Nthawi ina iwo anali ndi gulu la alaliki amenewo kunja monga choncho, mmbuyo mu Chipangano Chakale, kuwaphunzitsa iwo mulu wonse wa zinthu. Ine ndikuwonetsani inu chiyani—ndi mtundu wanji wa maphunziro omwe iwo

anali nawo. Iwo anali kuwaphunzitsa iwo zonse za fioloje za tsiku limenelo, sukulu ya aneneri. Ndipo iwo anabwera kuti adzamuwone mneneri weniweni tsiku lina. Mneneriyo anati kwa mmodzi wa iwo, "Pitani uko ndipo mukadzitolere inu chilolo chodzadza ndi—ndi chipere china tsopano, ife tidzayika pa ketulo yayikulu, ife tikakhala ndi a—mphika wawukulu wophikidwa wa nandolo kunja kuno."

118 Ndipo inu mukudziwa chimene mlaliki uja anachita? Iye anapita kunjako ndipo anakathyola chilolo chodzadza mphonda, mphonda zobiriwira kuchokera ku mpesa wakuthengo. Mnyamata, mnyamata yemwe sankadziwa kusiyanitsa pakati pa nandolo ndi mphonda zakuthengo, ndi mlaliki wina, ine ndikukuuzani inu. Iye anaponyera izo mu mphika ndipo anayamba kuphika izo. Chinthu choyamba inu mukudziwa, aliyense anali ndi mbale yaikulu yodzaza ndi izo monga choncho, ndipo anati, "Muli imfa mu mphika."

119 Ndiro limene liri vuto lero, muli imfa mu mphika! Ena a seminare yakale yozizira iyi, yofunda, malo opanda umulungu akupitirira, akuyesera kuphunzitsa fioloje ina. Iwo akuwang'amba anthu, kuwachotsa iwo kwa Khristu. Ife tikusowa ubatizo wa Mzimu Woyera kuti upereke Moyo. Aleluya! Psyii! Ine ndikumverera kuwirikiza kawiri kukula kwanga tsopano. Koma ndicho choonadi, m'bale, inu mukuphika chinachake. Ndiko kulondola, inu mukuphika chinachake, koma inu mukuphika chiyani? Ndicho chinthu chotsatira. Mnyamata yemwe samadziwa kusiyanitsa pakati pa mphonda zobiriwira ndi nandolo! Ndizo pafupifupi monga ena a iwo. Ndicho choonadi. Inde, bwana.

Anati, "Muli imfa mu mphika."

120 Elisha wokalamba anali mneneri weniweni. Iye anati, "Oh, musadandaule za zimenezo. Musati mukondowezeke yense." Ameni. Ife tiri naye munthu kuno yemwe ali ndi magawo awiri. Aleluya! Iye anali atawoloka ku dziko la Kenani, anali atabwerera, anapeza magawo awiri. Anati . . . Iwo amadziwa choti achite pamene vuto libwerapo. Anati, "Pitani mukanditengereko ine ufa wodzaza mdzanja." Iye anatenga ufawo ndikuwuponyera iwo mu mphika. Anati, "Tsopano idyani zonse zomwe inu mukufuna. Izo ziri bwino tsopano."

121 Chifukwa chiyani ufa? Ufa unali pamenepo kwa choweyula, kwa nsembe yaufa, nsembe-yoweyula pamaso pa Ambuye. Ndipo ufa umenewo unkayenera kuti uperedwe ndi mphero yomwe inkapera njere iliyonse mofanana. Nsembe ya ufa imeneyo inali Khristu. Kumuika Khristu mmenemo, mphero iliyonse chimodzimodzi. Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Pamene muli imfa mu mphika, ikani Khristu mmenemo. Aleluya. Psyii! Ulemelero! Aleluya!

122 Ine ndinamuwona poyamba winawake ali ndi Mzimu Woyera, anali mwamuna wachikulire wachikuda atavala chikhoto chachikulu, chachitali. Iwo ankayenera kumuthandiza iye (iye anali wokalamba kwambiri) monga *chonchi*, ndipo iye anafika pamwamba apo ndipo anayamba kulalikira. Ambiri a alaliki amenewo anayamba kulalikira za, oh, zomwe zinachitika kuno pa dziko lapansi. Iye anatenga mutu wake kubwerera mu Yobu, "'Kodi iwe unali kuti pamene Ine ndinkaika maziko a dziko lapansi, pamene nyenyezi za mmawa zinkayimba limodzi ndipo ana a Mulungu ankafuula mokondwera?'" Iye anati, "Inu mukuganiza kuti ife tiri ndi mtundu wina wa chipembedzo chatsopano." Anati, "M'bale, ine ndangokhala ndi nkhani yachikale, kapena nkhani yatsopano ya chipembedzo cha nthawi-yakale." Patapita kanthawi Mzimu Woyera unamugwira iye. Munthu wachikulire wosauka anali wowuma kwambiri, iye anali atayima pamenepo; iye anadziwongola yekha, anamenyetsa zidendene zake, pamodzi, ndipo anati, "Ulemelero! Aleluya!" Anati, "Inu mulibe malo okwanira pano oti ndilalikirepo," anayenda kuchoka pa nsanja.

123 Ine ndinati, "M'bale, ngati Iwo ungachite zimenezo kwa mwamuna wa usinkhu wa zaka eyite, kodi Iwo ungachite chiyani kwa ine? Ine ndikuwufuna Iwo!" Aleluya! Kulondola. Inde, bwana, ine ndinali ndi nthawi yopambana. Ndinapita kumene mmunda wa chimanga, ndipo pa mawondo anga akale a dzimbiri ine ndinapita, ndipo ine ndinali kuwupempherera Iwo. Uko nkulondola.

124 Monga Buddy Robinson wakale, anakhala akupitirirabe, ankafuna Mzimu Woyera. Anati, "Ulemelero kwa Mulungu! Ine ndinkafuna Mzimu Woyera moyipa kwambiri, ine sindinkadziwa choti ndichite." Iye anati, "Ine ndinali kulima chimanga m'mawa wina ndi Alec wakale," mphongolo yake. Anati, "Alec anapitirira kumaponda chimanga. Ine ndinamukwiyira iye, ndinathamangira kumeneko ndipo ndinakamuluma iye pa khutu mwamphamvu momwe ine ndikanathera. Alec anandikankha ine." Anati, "Ine ndinapita uko ndipo ndinakakhala pansi. Ine ndinayang'ana pa iye, iye anali atayima pamenepo." Anati, "Ine ndinamuluma Alec wokalamba momwe ine ndikanathera." Anati, "Ine ndinayang'ana pa iye, ndinati, 'Alec.'" Anati, iye anati, "'Alec, ine ndikupepesa. Ine sindidzachitanso izo aponso.'" Anati, "Alec anayang'ana pozungulira, anati, 'Iwe simupeza chipembedzo chochuluka kuposa chomwe inu muli nacho tsopano, inu mukanachita nane mwanjira imeneyo kachiwiri.'" Mai, mai! Uko nkulondola. Iye anati, "Ine ndinatsikira mu mzere wa chimanga, ndipo ndinati, 'Ambuye wabwino, ndipatseni ine chidziwitso chochuluka ku mapeto a moyo wanga. Ndithandizeni ine kulimbana ndi mdierekezi malingana ngati ine ndiri ndi dzino m'kamwa mwanga, ndiye nkumuluma iye mpaka ine ndidzafe.'" Iye anati,

"'Ambuye, ngati Inu simundipatsa ine Mzimu Woyera, pamene Inu muzidzabwerera ku dziko lapansi Inu mudzapeza mulu wa mafupa uli pomwe pano.'" Iye anawulandira Iwo. Ameni. Uko nkulondola.

125 Iwe umafika pansi kwenikweni ndi kutanthauza izo pamaso pa Mulungu, Mulungu adzakulandirani inu, ndi kuwoloka kumeneko. Ziribe kanthu zomwe alaliki aku seminare anena, ife tikhoza kukhala nawo Mzimu Woyera chifukwa Mulungu analonjeza Iwo kwa ife.

126 Ndiko kumene Kalebu anakhazikitsapo—anakhazikitsapo chikhulupiriro chake, ndi pamene Yoswa anakhazikitsapo icho, chifukwa Mulungu anati, "Ilo ndi lanu, ine ndalipereka kale Ilo kwa inu." Aleluya! Ine ndikuzikonda zimenezo. Osati "Ine ndidzatero." "Ine ndatero!"

127 "Iwo amene Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa." Ndi kulondola uko? "Ndipo iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa ulemelero." Ndi kulondola uko? Ndiye, m'bale, Kumwamba ife tinapatsidwa kale ulemelero limodzi ndi Khristu Yesu. Aleluya! Uko nkulondola. Mungomusiya mdierekezi alire mokweza ndi kukuwa ndi kukhala ndi zokwiyitsa zake zonse zomwe iye akufuna kutero. PAKUTI ATERO AMBUYE! Uko nkulondola. Oh, mai!

128 Tiyeni tifike kuno kwinakwake, kupita kukalalikira kwinakwake kumene iwe umachoka pa izo pang'ono pokha. Oh, zodabwitsa bwanji! Iwo amayamba kung'ung'udza pambuyo pake, kukangana. Tiyeni tipite cha pafupifupi mutu wa 21, ndi kuyambira pafupifupi ndime ya 5. Iwo anayamba kung'ung'udza pamenepo, ndi kukangana, kumapitirira; kudula madzi.

Mwinamwake ndiro limene liri vuto ndi mpingo usikuuno, kuchita kukangana kwambiri ndi kung'ung'udza pozungulira! Madzi adulidwa.

129 Inu mukudziwa, ine—ine ndimayenda kuzungulira padziko lapansi lonse kwambiri. Ndipo amodzi a malo obaya kwambiri, oyipa kwambiri oti uyesere kukhalapo, ndi m'chipululu. Chirichonse kumeneko chiri ndi chobaya pa icho. Inu mukudziwa chifukwa chake? Mtundu uliwonse wa udzu wakale ndi cactus. Iwe sungakhoze kugona paliponsepo, izo zimakubaya iwe. Chifukwa chake ndi chakuti, iwo alibe madzi. Madzi amapangitsa kuti zifewe. Kumene kuli madzi ambiri, inu simukhala ndi minga ndi nthula, kumene kuli madzi ambiri.

130 Ndipo ine ndikukuuzani inu, m'bale, inu mutenge mpingo wakale umene uli wowuma mu fupa lake, ndipo mulibe Mzimu Woyera mmenemo, ndipo mulibe chipulumutso, mulibe machiritso Auzimu, mulibe mphamvu ya Mulungu, mulibe kufuula, mulibe chisangalalo, ndipo zimatero nthawizonse, "*Izi*, oh, iye anachita *izi*, ndipo iye anachita *izi*, ndipo iye anachita *izi*," kubaya, kubaya, kubaya. Chimene inu mukusowa

ndi kutsanulidwa kwachikale kwabwino, kukhavukira, kwa Mzimu Woyera, aleluya, ndi kufewetsa pang'ono pokha. Ameni! Izo zimatanthauza "zikhale chomwecho." Branham Tabernacle akusowa mlingo wabwino wa izo, nayenso. Ndiko kulondola. Oh, ndi kulondola uko? Ameni! Oh, ine ndikukhala ndi nthawi yabwino kuno. Zovala zanga zikundikwanira ine ndendende basi, M'bale Higginbotham. Inde, bwana. Kolala yanga si yayikulu kwambiri, malaya anga akukwanira, ndikungomverera bwino. Ngakhale mkazi wanga sali kuno, kotero ine—ine ndikhoza kungokhala ndi nthawi yaulemelero. Oh, inu musamuwuze iye, ayi. Chabwino, koma ine ndikukhala ndi nthawi yabwino!

Inu mukuti, "Ndinu okondwa?"

131 Ndithudi, ndine wokondwa. Kodi ine ndingaleke bwanji kukhala wosangalala, ndikudziwa zomwe ine ndikudziwazi? Ameni. Khristu anandipulumutsa ine, anandidzaza ine ndi Mzimu Woyera, anandipatsa ine tikiti yopitira Kumwamba. Ine ndikungokhala ndi nthawi yopambana, ndikupitirira, ndikuti, "Kazibwerani, nonse a inu." Inde, bwana.

132 Zikundikumbutsa ine za mnyamata wina nthawi ina amene anapita kukayika nkhuku. Ndipo nkhuku yakaleyo inali nayo. . . Iye anali ndi mazira okwanira kuzikhazika zonsezo kupatula limodzi. Ndipo iye analibe. . . Iye anaganiza, "Kodi ine ndichita nalo chiyani dzira limodzi limenelo?" Kotero iye anapita kunja ndipo iye anakapeza dzira la bakha, ndipo iye analiyika ilo pansi pa nkhuku yakaleyo.

133 Ndipo nkhuku yakaleyo inaswa anapiye ake onse, ndi bakha, aponso. Ndipo iwo anali akuyenda pamenepo mu khola, inu mukudziwa. Ndipo ngati bakha wamng'ono wakaleyo akanapanda kuyang'ana kunja kwa malo ake; pafupifupi monga mmodzi wa inu oyera odzigudubuza tsopano, inu mukudziwa. Ankayenda pamenepo, "Kwaa-kwaa, kwaa-kwaa," monga choncho. Ndipo, oh, iwo amakhoza kupita kuseri kwa kholalo, inu mukudziwa, ndipo nkhuku yokalambayo imakhoza kugwira chiwala. Ndipo, "kwaa-kwaa, kwaa-kwaa." Apa iye ankapita, "Kuluka-kuluku, kuluku-kuluku." Ndipo apa panabwera anapiye aang'ono akuthamangira kwa iye monga choncho, mmodzi aliyense. Koma bakha wamng'onoyo sankadziwa kuti kuitana kwake kunali chiyani, "kwaa-kwaa." Iye sankadziwa chimene fumbi lonselo limatanthauza, ilo linalowa mu mphuno zake ndi chirichonse. Iye anali kanthu kakang'ono kowoneka-moseketsa, kuchokera kumalo ake.

134 Monga membala wabwino wachikale wa Mzimu Woyera mu mpingo wachikale wozizira wofunda, wochoka pamalo ake. Kuyankhula za zonse *izi*, *izo*, ndi *zinazo*, ndipo purezidenti ndi ndani. Iwo amafuna kudziwa Yemwe, Mulungu, iwo amafuna kudziwa za Mulungu.

135 Koma, inu mukudziwa, nkhuku yokalambayo inalakwitsa tsiku lina, monga momwe mpingo wakale unachitira. Uko nkulondola. Iyo inatuluka tsiku lina, inawulukira mmwamba momwe mu khola monga izo zinkayendera ndipo patapita kanthawi kabakha kakang'ono kakakulu kanakweza mutu wake mmwamba, ndipo, kananunkhiza, kananunkhiza, kananunkhiza, kananunkhiza, iye ananunkhiza madzi. Icho chinali chikhalidwe chake, inu mukudziwa. Ameni. Iye ananunkhiza madzi. Iye anati, "Honko-honko, honko-honko." Oh, mai! Iye sanali chikhalidwe cha nkhuku, mulimonse, iye anali chikhalidwe cha bakha. Kotero iye ananunkhiza madzi, apo panali kamtsinje kamene kamatsikira kumusi kumeneko. Nkhuku yakaleyo inafuula, "Kuluku-kuluku, kuluku-kuluku, kuluku!"

Iye anakuwa, "Honko-honko, honko-honko," akupita molunjika kumadzi mwamphamvu momwe iye akanathera.

136 Umo ndi momwe izo zimakhalira ndiye pamene munthu abadwira mu Ufumu wa Mulungu. Mpingo wakale ukhoza kunena kuti, "Inu muchoke kwa oyera-odzigudubuza awo, ndi zamkhutu, ndi *izi*, *izo*, *zinazo*." "Honko-honko, honko," iye akuyenera kuti akafike kumadziwo! Aleluya.

137 Ulemelero! "Iye amene akhulupirira ndipo abatizidwa adzapulumutsidwa." Ulemelero kwa Mulungu! Inu mukuti ndi misala; koma, m'bale, ndife okondwa!

138 "Honko-honko, honko-honko, honko-honko." Abakha aang'ono amenewo anayamba kupita kumadzi. Chinali chiyani chimenecho? Icho chinali chikhalidwe chake. Iye sakanakhoza kuchitira mwina. Munali chinachake mwa iye, chikumuyitanira iye ku madzi.

139 Ndipo pamene Mulungu ali mu mtima, izo zidzakuitanirani inu ku msonkhano-wakachitidwe kachikale, wa Mzimu Woyera. Ulemelero kwa Mulungu! Ulemelero! Ndiko kulondola, m'bale, ine ndikudziwa ndi chikhalidwe changa. Aleluya! Pokhapokha ngati chikhalidwe chanu chasinthidwa, inu mudzamvetserabe kulira kwa nkhuku yakale. Koma pamene inu mununkhiza madzi, ngati inu muli bakha, inu mukuyendayenda, chifukwa inu mwalunjika wa ku madziwo. Aleluya!

140 Yoswa anati, "Ah, ife tikhoza kukwanitsa izo." Yoswa anati, "Ife tikhoza kuchita izo." Kalebu anati, "Ife tikhoza kuchita izo."

"Inu mukudziwa bwanji kuti ife tikhoza kuchita zimenezo?"

141 Iye anati, "Chifukwa Mulungu wanena chomwecho, ndipo ife tikupita kumeneko. Ife tikupita kukachita zimenezo, ndipo ife tikachita zimenezo." Ndipo kutali iwo anapita! Iwo ananyamuka wopita ku dzikolo, ndipo iwo analandira umboni wa Mzimu Woyera, ndipo iwo anabwerera kudzatsimikizira izo. Dzikolo linali labwino, linali kubala mphesa zabwino. Ndine wokondwa ndi zimenezo, sichoncho inu? Oh, mai, ingowadyani

iwo ndi kumachucha dovu ngati kavalo akudya nkhanu. Ndiko kulondola. Inde, bwana, kungokhala ndi nthawi yopambana, kusangalala.

142 Kodi ndikusamala chiyani zomwe dziko likunena? Palibe kanthu kwa ine. Mulungu yemweyo amene anandidzutsa ine, amene anapulumutsa moyo wanga, ndipo ananditumiza ine cha kuno, kudzapempherera mafumu ndi china chirichonse, kudutsa dzikoli. Iwo unali Mzimu Woyera wabwino wa kachitidwe-kachikale uwu umene unachita zimenezo. Ine sindinayambe ndachitapo nawo Iwo manyazi. Ine ndanenapo mu nyumba zachifumu, "Ine ndinalandira ubatizo wa Mzimu Woyera." Aleluya. Uko nkulondola. Iwo ali ndi njala, nawonso. Iwo akuchita njala ndi ludzu.

143 Penyani apa, iwo anayamba kung'ung'udza ndipo anayamba kudandaula. Madzi anadulidwapo.

144 Tsopano fulumirani. Kodi ife tiri ndi nthawi yanji? Ndikuti, ine ndikupepesa, ine ndachedwa. Mundikhululukira ine chifukwa chophunzitsa motalikitsa kwambiri. Oh, sindinaphunzitse panobe, ndatero ine? Koma miniti yokha, ine ndifika ku phunziro langa pakapita kanthawi. Ayi, ine ndimangokuseleulani inu, khalani chete. Tiyeni tingotenga mawu pang'ono apa, ine ndiri ndi chinachake ine ndikufuna kuti ndinene.

145 Ndime ya 5 ya mutu wa 21 tsopano, ndipo mvetserani mwatcheru kwenikweni.

> *Ndipo anthu anayankhula motsutsana ndi Mulungu, ndi motsutsana ndi Mose,* Ndikuti *kumene iwe watibweretsa ife* kudzalowako, kuchokera ku *Igupto* . . . kupita *ku chipululu* ichi? . . . kumene kulibeko *madzi; ndipo—ndipo* miyoyo *yathu ikunyansidwa ndi mkate wopepuka uwu.*

146 Atadzazidwa ndi chakudya chabwino cha Angelo ndi chirichonse, iwo anati, "Oh, ife tatopa nazo zimenezo. Ife tikufuna kukhala ndi gariki wina ndi maungu ena." Iwo ankafuna miphika yakale ya nyama ya ku Igupto.

> *Ndipo Ambuye anatumiza njoka zamoto pakati pa anthu, ndipo . . . kuwaluma anthuwo; ndipo anthu ambiri . . . anafa.*
>
> *Chotero . . . anabwera kwa Mose, ndipo anati, Ife tachimwa,* ndipo *ife tayankhula motsutsana ndi Ambuye, ndi motsutsa inu; pempherani kwa Ambuye kuti iye achotse kwa ife njoka* zamoto. *Ndipo Mose anawapempherera anthuwo.*
>
> *Ndipo Ambuye anati kwa Mose, Panga . . . njoka yamoto, ndipo uyike iyo* pa *mtengo: ndipo zidzafika*

*pochitika, kuti mmodzi aliyense amene alumidwa, pamene iye ayang'ana pa iyo, adzakhala ndi moyo.*

*Ndipo Mose anapanga njoka* kuchokera *ku mkuwa, ndipo* iye *anaika iyo* pa *mtengo, ndipo kumachitika, kuti ngati a—ngati njoka iluma munthu, pamene iye ayang'ana pa njoka ya mkuwa, iye amakhala ndi moyo.*

147 Oh, ndiroleni ine nditenge zimenezo, kanthu kakang'ono ako apo ife tisanalowe mu msonkhano wa mawa usiku. Njoka ya Mkuwa. Monga Thanthwe lomwe linakanthidwa usiku watha, pamene ife tinathera pa Thanthwe lokanthidwa; Njoka ya Mkuwa inali Yesu Khristu.

Inu mukuti, "Njoka?" Inde.

148 *Njoka* inkaimira "tchimo loweruzidwa kale." Mulungu anaweruza serpenti mmunda wa Edeni, mu mutu wa 3 wa Genesis, ndi ndime ya 14, Mulungu anapereka kale chiweruzo pa Njoka. Oh, iye anali wokongola, ndipo ankayenda wowongoka, iye anali wochenjera kwambiri mwa zirombo zonse za kuthengo. Koma Mulungu anamuweruza iye, ndipo anamugoneka iye pansi pa mimba yake kwa masiku ake onse, pa mimba yake. Anaweruzidwa!

149 Ndipo Khristu anali "machimo athu anaweruzidwa." Ameni. Inu mukuwona zimenezo? Zokongola. Tchimo langa, machimo anu, mwachirungamo ayenera kupita ku gehena ndi kukalangidwa chifukwa cha machimo athu. Koma Khristu anatenga malo athu. Njoka, ndi chifukwa chake iyo inkaimira Khristu.

150 Mkuwa, serpenti kukhala yopangidwa kuchokera ku mkuwa, zinkatanthauza "chiweruzo Chaumulungu." Tsopano, *serpenti* anali "tchimo loweruzidwa kale," ndipo *mkuwa* unkatanthauza "chiweruzo Chaumulungu."

151 Monga guwa la mkuwa. Guwalo linkapangidwa kuchokera ku mkuwa, umene unkawotcha matupi a nsembe. Eksodo mutu wa 17 inu mukazipeza zimenezo, ndiye, inu amene mukulemba Malemba anu.

152 Tsopano, iwo ankatenga chinyama, iwo ankachitsuka icho (choyimira changwiro, ubatizo), ankabweretsa icho mmenemo, ankayika manja awo pa icho (ankavomereza machimo awo), ankadula khosilo. Magazi anali. . .magazi ankakhetsedwa, ndipo nyama inkawotchedwa, pa magazi pa chipika chochitira nsembe, pa guwa, guwa la mkuwa, pamene machimo ankakanidwa, kumene iwo. . .kumene Mulungu wolungama ankafuna kulekanitsa kwathunthu. Ndipo chiweruzo Chaumulungu cha Mulungu, ndi moto, chinkawotcha nsembe ya tchimo. Aleluya.

Chiweruzo Chaumulungu cha Mulungu chinali pa Yesu Khristu.

153 Penyani, chiweruzo Chauzimu kachiwiri mmasiku a Eliya, zikusonyeza kuti icho ndi chiweruzo Chauzimu. Eli-. . . Inafika nthawi imene kunalibe kalikonse, anthu anali atachoka kwa Mulungu. Ndipo Eliya anakwera pa phiri, ndipo iye anapemphera. Iye anadza pamaso pa mfumu, ndipo anati, “Ngakhale mame sadzagwa kuchokera kumwamba kufikira ine nditawaitanitsa iwo.” Ndipo kwa zaka zitatu ndi miyezi sikisi, mame sanagwe ngakhale pa dziko lapansi.

154 Ndipo pamene izo zinafika pa malo, Eliya anati, “Tiyeni ife titsimikizire Yemwe ali Mulungu, Mulungu wamoto.” Mulungu wathu ndi Moto wonyeketsa. “Mulole Mulungu amene amayankha ndi moto.”

155 Ndi zomwe ine ndikunena usikuuno. Mulole Mulungu yemwe amayankha ndi Moto, Mzimu Woyera ndi Moto, msiyeni Iye akhale Mulungu!

156 Tsopano iwo amaika. . .Penyani, iye anakwera mmwamba atatha kutulutsa moto kuchokera kumwamba, ndi zina zotero, ndipo anali atanyeketsa nsembe, iwo anayang’ana kumwamba mu mlengalenga, ndipo imo munawoneka ngati mkuwa. Chinali chiyani chimenecho? Chiweruzo chauzimu pa fuko lonse.

157 Ndipo m’bale, mlongo, ngati inu mungayang’ane pozungulira lero, inu mudzawona mtundu wa mkuwa kachiwiri. Chiweruzo Chauzimu chikubwera pa fuko. Chiweruzo! Njoka yamoto, njoka zamoto, chiweruzo Chauzimu mmenemo.

158 Tsopano penyani, iye ankakweza mmwamba mtengo uwu umene unali ndi—njoka pa iwo, yopangidwa ndi mkuwa. Ndipo aliyense amene ankayang’ana pa serpenti imeneyo, amachiritsidwa ku matenda awo.

159 Ndi chithunzi chokongola bwanji usikuuno cha Yesu Khristu! Iye anati, “Monga Mose, monga Mose anakweza njoka ya mkuwa mu chipululu!” Ndi izi apa, tsopano mumvetse zimenezo. Ngati inu mukudwala, inu mupeza chomwe chingakuchiritseni inu. Monga Yesu ananena, “Monga Mose anakweza mmwamba njoka ya mkuwa mchipululu, koteronso Mwana wa munthu ayenera kukwezedwa mmwamba.” Chifukwa chomwecho, [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. mu chifukwa chapawiri, [Malo osajambulidwa pa tepi.] “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tachiritsidwa.”

160 Iwo anali kung’ung’udza motsutsana ndi Mulungu, ndi motsutsana ndi Mose, ndipo ankalumidwa ndi njoka. Njoka inasamalira ntchito ziwiri. Choyamba chinali kukhululukira tchimo lawo, ndi kuchiritsa matenda awo.

Ndipo Yesu anakwezedwa mmwamba kuti Iye akakhoze kukhululukira machimo athu, ndi kuchiritsa matenda athu.

161 Chotsatira paulendo, zitatha zimenezo panadzabwera Balaamu, mneneri waganyu, anabwera kumeneko kuti adzaimitse Israeli. Oh, mai! Ife tidzalowa mu zimenezo mawa usiku, momwe kuti munthu ameneyo. . .Ndipo mphongolo yosayankhula inachita kuyankhula ndi kumudzudzula iye. Mlaliki kuchoka ku chifuniro cha Mulungu, ndipo maganizo ake pa ndalama, anapita kumusi kumeneko, ndipo mphongolo inachita kumudzudzula iye kumusi uko, mphongolo yosayankhula. Ngati Mulungu angakhoze kuyankhula kudzera mwa mphongolo yosayankhula, ndithudi Iye akanakhoza kudzera mwa munthu! Inde, bwana.

162 Zindikirani pamenepo, Mose wokalamba wosauka, itatha nthawi yonseyo. Ine ndikufuna kuti ndikusonyezeni inu chimene munthu ali pamaso pa Mulungu. Momwe Korah ndi onse amenewo. . .Taonani pamene Mulungu anamuwuza Mose, "Choka pa njirapo, Mose, Ine ndiwononga gulu lonselo la iwo, ndipo ndipanga mwa iwe fuko lamphamvu."

163 Ndipo Mose anadziponyera yekha pamaso pa Mulungu, namanga mlatho njira yake, ndipo anati, "Mulungu, munditenge ineyo!" Ndipo Mulungu sakanakhoza kumuwoloka munthu ameneyo, mphamvu ya woyera pamaso pa Mulungu. Tayang'anani pamenepo.

164 Tayang'anani pa Yesaya wokalamba, akupita ku ntunda uko ndi kukamuuza mneneri Hezekiya, "Konzani nyumba yanu mwadongosolo, inu mufa. PAKUTI ATERO AMBUYE."

165 Zinali zochititsa manyazi bwanji, mu maora angapo, anadzabwerereranso kachiwiri. Mzimu Woyera unakomana naye iye. Chifukwa, Hezekiya anatembenuzira nkhope yake ku khoma ndipo analira mwamphamvu, ndipo anati, "Ambuye, ine ndikukupemphani Inu kuti mundiganizire ine. Ine ndayenda pamaso panu, ndi mtima wangwiro." Ndipo misozi ikuyenderera pansi pa tsaya lake. Ndipo Mulungu anali atasindikiza kale chiwonongeko chake, koma pemphero linasintha zinthu.

Iye anati kwa mneneriyo, "Bwerera ndipo ukumuuze iye."

166 Taonani momwe Mose analiri wankhondo! Mu maora ake otsiriza, iye anafika kumusi uko ndi kupsya mtima kumeneko, ndipo potsiriza anadzilemekeza yekha mmalo mwa Mulungu, ndipo Mulungu sanamulole iye. . .Zoona, izo zonse zinali zofaniziridwatu monga momwe mabungwe lero, Amethodisti, Abaptisti, Achipentekoste, ena onse a iwo, iwo akudzipatsa okha ulemerero.

167 Masiku angapo apitawo, umodzi wa mipingo ikuluikulu, basi chifukwa chakuti iwo sakanakhala bakha yekhayo mu chithaphwi, iwo amagwera pansi pa msonkhano monga choncho. Ine ndinati, "Ine sindikusowa kuchita kukhala ndi mgwirizano wanu. Kumene mphungu ziri, nyama-. . .kumene kuli nyama, mphungu zidzasonkhanako." Ndipo izo zinali zoona. Inde,

bwana. Inu muzingonena Choonadi, Mulungu adzasamalira zina zonsezo.

Ndipo iwo anali pamenepo, "Oh, ndife olamulira."

168 Ine ndinati, "Ine sindikusamala chimene inu muli. Mulungu ndiye Mmodzi wolamulira mmiyoyo yathu." Uko nkulondola. Izo zimatengera Mulungu, osati chimene mpingo ukunena. Ndipo mpingo, umodzi uliwonse wa iyo . . . Wazambiri yakale aliyense pano akulolera kuti ayang'ane izi. Uko kunalibe konse mpingo umene unayamba wagwa umene unawukanso konse. Mulungu amawayika iwo pa alumali. Iwo sanatero. Achilutera anagwa, Amethodisti anagwa, Apresbateria, Abaptisti, monse kudutsa, ndi Achipentekoste, nawonso. Mulungu amangowaponyera iwo mmbuyo pa alumali.

169 Ndipo ngati—ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu, inu muzimvetsera kwa izi. Ndipo ine ndikunena izi ndi kudzoza. Osati ndendende tsopano, koma zomwe zinabwera izi zisanachitike; kuti sipadzakhala bungwe limodzi loyimiridwa (la, chimene ine ndikutanthauza, bungwe lonse) kulowa mu Ufumu wa Mulungu; koma Mulungu adzakoka kuchokera mwa aliyense wa iwo, zonona za mbewu, ndi kuzidzaza izo ndi Mzimu, ndi kutengera icho ku Ulemelero. Izo nzoona.

170 Baibulo limaneneratu kuti m'badwo wa mpingo wotsiriza ndi M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya, umene uli wofunda. Ndipo ndizo basi molingana ndi momwe mpingo wafikira lero. Uko nkulondola. Iwo anafika pansi pamene mwina iwo akhoza kuwomba manja mwawo pang'ono, ndi kupanga phokoso pang'ono, ndi kulumpha mmwamba ndi kukankha mipando kwa kanthawi. Koma pamene izo zifika pakukhala moyo wangwiro, woyera, wosaipitsidwa, woyeretsedwa, iwo ali kutali monga momwe usiku uli ndi usana. Uko nkulondola. Chimene ife tikusowa lero ndi kufa kwa kachitidwe-kachikale, m'bale; kumene izo sizikubwerera ku guwa ndi kuyambiranso, ndi kubwerera ku guwa kachiwiri, kubwerera ku guwa. Kupita kumeneko ndi kukakhala mpaka inu mutafa, ndiyeno munthu wakufa samadziwa kanthu za mdziko. Aleluya! Sindikufuna kuti ndiyambenso pa izo. Taonani, m'bale, ndiroleni ine ndikuuzeni inu.

171 Mulungu, atatha kukhala ndi mtumiki Wake wosauka wakale, Mose . . . Winawake ananena kwa ine nthawi ina, anati, "Ine ndikukuuzani inu, izo zikusonyeza Mulungu, ngati inu mumamutcha iye Mulungu." Anati, "Iye anamutsitsa mtumiki wakeyo. Atatha . . . "

172 Moyo wa Mose umayenda mozungulira zaka forte. Iye anaitanidwa, ali forte, ndipo anakanidwa ndi abale ake. Anapita ku chipululu ndi kumakaweta nkhosa kwa zaka forte. Pamene iye anali ndi zaka eyite, Iye anamutumiza iye uko kuti

akawombole Israeli ku Igupto. Ndipo pamene iye anafika pafupi ndi dziko lolonjezedwa, iye anali usinkhu wa zaka handiredi ndi twente zakubadwa. Iye anali nako kuyenda kwachinyamata, ndipo kupenya kwake sikunamulepherepo iye, ndiko kulondola, pa handiredi ndi twente.

173 Koma pamene iye anadzipatsa yekha ulemelero kumusi uko, mmalo mwa Mulungu, pamaso pa Thanthwe limenelo; pamene Mulungu anamuuza iye, anati, “Pitani, ukayankhule ndi Thanthwe. Usakalikanthe Ilo. Ukayankhule kwa Ilo.” (Thanthwelo linangokanthidwa kamodzi kokha.)

174 Ndipo Mose anakwiya kwambiri, ndipo anathamangira kumeneko ndipo anakantha Thanthwelo. Ilo silinabweretse madzi. Iye analikankha Ilo kachiwiri, Ilo linabweretsa madzi. Anati, “Inu opanduka, kodi ife tikutulutsireni inu madzi kuchokera mu Thanthwe ili?” Monga choncho, ndipo anatulutsa madziwo, chifukwa Mulungu ankayenera kumumvetsera mneneri ameneyo chifukwa Iye anamulonga iye ndi mphamvu imeneyo. Ndipo izo zinaswa dongosolo lonse la Baibulo la Mulungu.

175 Khristu anakanthidwa kamodzi. Ife tikuyankhula kwa Thanthwe tsopano, ndipo Ilo likutulutsa madzi Ake, mwaona. Ilo linamenyedwa kale. Ukangoyankhula kwa Ilo, ndipo Ilo litulutsa madzi Ake.

176 Tsopano, ine ndinamuwona iye mmawa umenewo. Oh, pamene ine ndikuganiza za chithunzi ichi, mtima wanga pafupifupi umandilephera ine. Ine ndikumuwona Mose, iye ankadziwa. . .Mulungu anati, “Mose, uwauze iwo zonse ‘motalika kwambiri,’ osonkhana ako. Ine ndikuitanira iwe pamwamba pang’ono tsopano, lero.”

177 Ine ndikukhoza kumuwona Mose wachikulire atayima pamenepo, ndevu zazitali zaimvi zimenezo, ndipo tsitsi lake likugwera pansi kuzungulira nkhope yake, maso ake akale akutsinzina ndi misozi, pamene iye amayang’ana pa omvetsera ake. Momwe iye anagwera pa . . . Momwe iwo anang’ung’udzira, ndi momwe iye anawaimirira iwo. Iye anawayang’ana iwo paliponse. Iye anayamba kuyenda kukwera phiri. Iye anakwera pamwamba pa phiri, iye anatembenuka mozungulira, iye anayamba kugwedeza tsalani-bwino kwa iwo. Iye anakwera mmwamba, mpaka pamwamba pa phiri. Unali mwezi wa Epulo. Iye anayima ndipo anayang’ana mdziko lolonjezedwa. Oh, momwe iye ankafunira akanapita kumeneko! Mai, mtima wake wakale wosauka unali ukusweka. Iye ankafuna akanapita ku dziko lolonjezedwa ndi gulu lija la Ayuda amene iye anali atawatsogolera ndipo anaima panjira. Ndipo apo iye anali, iye anayang’ana cha kumeneko, ndipo misonzi ikuyenderera pansi pa masaya ake. Iye anatembenuka ndi anagwedezera kwa anthu kachiwiri, tsalani-bwino, abusa awo akale. Iye anali

akupita kutali. Iye anawagwedezera iwo monga *choncho*. Iye anayang'ana mmbuyo.

178 Ndipo kokha ngati ine ndingaime pamene Mose anaima ndi kuwona mawonekedwe a malowo! Mulungu akalola, mmiyezi ingapo yotsatira, ine ndikufuna kuti ndidzayime pa phiri pamenepo ndi kudzayang'ana pamene iwo anawoloka.

179 Ine ndinawona kanema tsiku lina, pamene ena a abale, pafupifupi forte a abale anga ochokera mmisonkhano yokopa anthu, mmenemo, anapita kumeneko, ndipo iwo anatenga sewero la kanema la zimenezo. Ndipo pamene iwo anawoloka pamenepo, anthu amenewo akukuwa ndi kufuula, ankafuna ngati agwetsere pansi tchire lonse pa gombepo, kumene ana a Israeli anapita kuntunda uko, kumene Yesu anabatizidwako. Ndipo mmodzi aliyense wa alaliki amenewo analumphira mmadzi, atavala zovala ndi zonse, ndipo anabatizana wina ndi mzake kachiwiri, mmodzi aliyense wa iwo. Oh, m'bale, muli chinachake mmenemo chosuntha ndi kukondoweza. Ife tikukhala moyo. . .Iwo amalowa mgalimoto, iwo amakhoza kukwera kachidutswa kakang'ono, ndi kunena, akubwera pa ulendo umenewo uko kumene ana a Israeli anatero. Monga Buddy Robinson wakale anati, "Imitsani chinthu ichi, mwamsanga ndithu!" Ndipo iye anatuluka panja ndipo anathamanga nkuzungulira, ndi kudzazungulira, ndi kuzungulira, akufuula pozungulira malowo, ndi kumakuwa, "Ulemelero kwa Mulungu! Aleluya!" Analumphiranso mkati, anati, "Muyendetseni iye." Uko nkulondola. Iye akungokhala ndi nthawi yoteroyo! Ndithudi!

180 Ngati ndingakhoze kuyima pamene Mose anayima, pa Thanthwe limenelo, kuyang'ana uko mdziko lolonjezedwa! Iye ankafuna kupitako, ndipo iye anayang'ana mmbuyo kwa osonkhana ake, anadzawa-baibitsa iwo kachiwiri. Misozi ikutsikira pa ndevu zake zazitali. Ora lake linali likubwera. Mikono yake, inadutsa mmikono yake apa, kugunda kunayamba kukwera mmwamba, msilikali wakale.

181 Ine ndikhoza kukuuzani inu pakali pano, m'bale, musaganize kuti ine ndikupita nazo izi kwa "Abaptisti" pang'ono pokha, koma, m'bale, iye sanataike. Ayi, iye sanatero. Mulungu sangamukhumudwitse mtumiki Wake.

182 Kumeneko mikono ikukwera monga *chonchi*. Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, iye anagwidwa, kugunda—kugunda kozizira. Maso ake anayamba kuchita mdima pamene iye ankayang'ana cha kumeneko, ku dziko limenelo. Momwe iye ankafunira kuti apite kumeneko! Oh, mai! Mtima wake unali kusweka.

183 Ndipo basi atangokonzeka kuti achoke mmoyo uno, iye anapezeka kuti anayang'ana, atayima pambali pake, apo panadzayima Thanthwe. Kungoti Iye ali pamenepo,

ndizo zonse. Iye anaponda pa Thanthwe. Angelo anabwera, anadzamunyamulira iye kutali.

184 Zaka eyiti handiredi kuchokera kumeneko, apo iye anali atayima uko mdziko lolonjezedwa, pambali pa Eliya, akuyankhula ndi Yesu. Iye samakukhumudwitsa iwe.

185 Ena a masiku awa ine ndiyenera ndidzabwere kumapeto a msewu. Ndine wausinkhu wa zaka forte-firii tsopano, ndikuyamba kusweka kwambiri. Ine ndalalikira zaka twente. Ine ndadutsa mmadzi ndi kuswa ayezi, ndipo ndayimapo ndi kubatiza mpaka ine kuzizidwa, pafupifupi. Ine ndachitapo opanda, kupita opanda, mu nkhalango ndi china chirichonse, ndipo matenda ndi chirichonse zikubisalira. Ine sindikudziwa kuti ine ndikhala nthawi yayitali bwanji. Koma ngati ine ndingakhale moyo kuti ndiwone motalika kuposa izi, mwinamwake pamene ine ndidzafike pokhala bambo wokalamba, ngati Yesu achedwa, ine mwinamwake ndidzaima ndi tsitsi lomwe ine ndiri nalo likulendewera pansi. Anthu anga onse amafooka pamene iwo akukalamba, iwo amanjenjemera. Pamene ine ndamenyera njira yanga kudutsa nkhondo iliyonse, azimzanga onse ndi zinthu atapita, ndipo ine nkudzayima pamenepo ndi kumamva kuthamanga kwa madzi akubwera kumeneko, ine ndikunjenjemera pa ndodo yanga, monga *chonchi*, Ine ndikufuna ndidzanyamule Lupanga lakale apa ndi kudzalibwezeretsa ilo mchimake cha Muyaya, kudzavula chisoti changa ndi kudzachiyika icho pansi, kudzakweza dzanja langa, aleluya, ndi kumati, "Ambuye, ndikankhireni kuno Ngalawayamoyo, ine ndikubwera kumeneko mmawa uno, ndikubwera kudzawoloka mtsinje." Iye sadzandikhumudwitsa ine pamenepo.

186 Ndipo pamene ine ndiri kuno, pamene kukadali kowala, ine ndizilalikira ndi kupemphera, ndi kupempha ndi kuyimba, ndi kuchita chirichonse chimene ine ndingathe ku Ufumu wa Mulungu. Pamene moyo wanga udzayamba kukanganuka kuchoka mthupi ili, ndipo ine nkudzayang'ana mmbuyo pansi ndi kudzawona mphondero zanga, ine ndikufuna iwo adzakhale pamalo a mtundu wabwino, komwe, "Kusiyana kumasiya mmbuyo mwathu mphondero pa mchenga wa nthawi."

Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Teddy, pita ku limba kamphindi.

187 Atate athu Akumwamba, oh, chifukwa cha nthawi zazikulu zokondweretsa izi, ndi zokondwa bwanji! Ine ndikuganiza ine ndimabalalika pang'ono pokha, Ambuye, Mzimu Woyera basi ukungobatiza moyo wanga. Ine basi sindingakhoze kuzithandiza izo, Chinachake chimangondigwira ine. Ndine wothokoza kwambiri, Ambuye, kukhala ndi mbale zonse ndi ngalande zitatsukidwa, kuti Mzimu Woyera ukhoze kubweramo. Muchotse zovuta zotsekereza mu payipi, kuti madzi a chipulumutso akhoze

kutsanulidwamo nthawi iliyonse imene Mulungu angafune kuti Iwo atero. Zipempherani momveka. Monga Elisha anamuwuza Yehosafati, ndipo anati, "Kumbani maenje. Chotsani miyala yonse, mitengo yonse ndi zitsa. Pakhala pali madzi ena akubwera."

188 Zikomo Inu, Ambuye, Inu mwakhala muli pano usikuuno. Ndipo ine ndikuganiza za mneneri wakale Mose, Mulungu, mudalitse moyo wake wochirimika, pamene iye anayima pamenepo pa phiri, akuyang'ana uko mdziko lolonjezedwa, ife taima usikuuno tikuyang'ana mbali imeneyo, Ambuye. Chinthu chokhacho chimene ine ndikukupemphani Inu, kwa inemwini, ndi kulola kuti Thanthwe limenelo lidzakhale pamenepo pamene ine ndizidzapitako. Mulungu, izo zidzakhala zabwino ndi ine. Ndipo zonse zimene ine ndinayamba ndazichitapo mmoyo, Ambuye, ngati ine ndingakhoze kudzangokwawira mmwamba ndi kudzakhudza mapazi Anu opatulika, kamodzi, kuwasisita iwo ndi dzanja langa losayenera, izo zidzandibwezera ine nthawi millioni. Ife tonse tikudziwa kuti ife tidzayenera kupita njira imeneyo. Ena a ife mwina titero mu ma ora pang'ono. Ine sindikudziwa. Inu mukudziwa.

189 Pamene ife tiri pano usikuuno, Atate, ndipo Mzimu Woyera ukadalipobe (wakhala uli pano ukudalitsa anthu Anu), Atate, ine ndikukupemphani Inu chinachake. Kodi alipo winawake pano yemwe ali wosapulumutsidwa, Ambuye, amene sakukudziwani Inu ngati Mpulumutsi wawo, samadziwa momwe iwo akuyimira pamaso Panu? Ine ndikufunsani Inu, Ambuye, ngati Inu mungatero. . . Osati kuti anthu awa andimve ine tsopano, koma ine ndikufunsani Inu ngati Inu mungangoyankhula kwa mtima umenewo ndi kuwapatsa iwo kulimbika mtima usikuuno.

190 Kukhoza kukhala kuyitana komaliza. Ife tingadziwe bwanji? Bwanji kutenga mwayi pamene Muyaya wonse uli pa Izi?

191 Ngati pangakhale, Ambuye, kapena m'modzi wosochera, wakuchoka pa Njirayo, akhoza kukhala kuti akukwera phiri kuti akayang'ane mdzikolo, ndiyeno nkukakanidwako. Mulungu, mulole Thanthwe likakhale ndi iwo, ine ndikupemphera. Tithandizeni ife tsopano, ndipo mudalitse omvetsera awa pamene ife tikudikirira.

192 Tsopano, ngati muli mwamuna kapena mkazi muno, mnyamata kapena mtsikana, ndi mutu wanu woweramitsidwa. . . Ndipo wina asayang'ane mmwamba, chonde. Anthu amakhala amanyazi kwambiri, nthawizina, amakhudzidwa ndi izi, koma njonda ndi azimayi.

193 Ine ndayenda kale wochuluka—mtunda wochuluka kumbuyo kwanga, mu zaka forte-firii izi. Masiku pang'ono chabe apitawo, ine ndinali mnyamata wamng'ono wachikulire ndikuthamanga kuzungulira kuno, ndikusewera mabulo ndi inu. Chabwino,

ine ndikulephera. Ine ndikukhoza kuzimverera izo. Ine—ine ndayesetsa kwa zaka twente, kuyesetsa kuti ndibweretse kwa inu Chinachake.

194 Jeffersonville, chifukwa chiyani inu mukuchikana Icho? Pamene Mulungu wachitsimikizira Icho, anatumiza Mngelo Wake, anajambula chithunzi cha Icho, Icho chikudziwika kuzungulira dziko lapansi, bwanji inu mukuganiza kuti Icho chinali mtundu wina wa a—chinachake chodzipangitsa-kukhulupirira?

195 Kodi mulibe Mulungu usikuuno? Inu mungakonde mutamudziwa Iye, kwenikweni. Inu mukudziwa kuti inu mukufuna chipulumutso cha mtundu umenewo inu musanafe.

196 Kuno nthawi ina kale, mu mzinda womwewu, kunali mtsikana wamng'ono anali wa mpingo winawake kuno mu mzinda, iye ankaganiza kuti iye anali wabwino. Abusa ake anamuuza iye kuti iye anali wabwino. Iye ankamuseka mtsikana wamng'ono akamabwera ku tchalitchi, chifukwa iye samapita ku kanema. Iye anati, "Abusa ako ndi a malingaliro-owonda."

Mtsikana wamng'onoyo anati, "Izo ziri bwino."

197 Patapita kanthawi iye anayamba kumayenda ndi gulu loyipa, ndipo anatenga matenda ndipo anazisiya izo zipite patali kwambiri. Adokotala, dokotala winawake wa mzinda uno, anapita kuti akamupime iye; atapitako anakapeza kuti, iye anali atadyedwa ndi chindoko. Iye anamwalira zitachitika zimenezo. Iwo. . .Iye anali mphunzitsi wa Sande sukulu mu mpingo waukulu uwu. Iwo onse anali kunja uko, ndi kumuwona iye akupita Kumwamba. Ndipo basi nthawi yomweyo, kalasi yake ya Sande sukulu inalowa. Abusa ake akutuluka mu holo, akusuta ndudu. Ndipo pamene inali nthawi yoti iye azipita ulendo wake, Angelo kuti abwere, adzamutenge iye; iye anadzuka, iye anati, "Abusa ali kuti?" Iwo anapita ndipo anakawatenga iwo. Iye anati, "Iwe wonyenga anthu!" Anati, "Ndi chifukwa chiyani iwe unandilola ine kukhala mumkhalidwe wotere? Ine ndataika!"

198 Musadandaule, Adamu anadziwa kuti iye anali ndi masamba a mkuyu pamene iye anabwera pamaso pa Mulungu. Izo zinali zabwino pamene Mulungu anali asanafike pafupi. Anati, "Ndi chifukwa chiyani inu munandilola ine kumapita monga chonchi?" Anati, "Ali kuti mtsikana wamng'ono wakale uja wochokera ku kachisi uko?"

"Oh, iye. . ." Iye anati, "Iwe—iwe—iwe wabalalika, ndikawaitana adokotala kuti akupatse zotontholetsa."

Iye anati, "Iwe wonyenga anthu! Ine ndataika, ndipo moyo wanga ukupita ku gehena, chifukwa cha iweyo." Iye anaweramitsa mutu wake.

199 Ndipo mzanga wabwino wa ine amagwira ntchito kuno mu galaja pakali pano, anali kugwira ntchito kwa oyika maliro.

Iwo anatsikira kumeneko kuti akamupopere zimankhwala mthupi mwake, ndipo iye anakhala akupopera, iwo amakhala akumamva fungo la mankhwalawo, ndipo samakhoza kudzaza mitsempha yake, ndipo anabwera kudzakokera zovala zake pansi, ndi kuyang'ana, ndipo pamenepo panali bowo lodyeka mthupi lake pamenepo lalikulu ngati chibhakera chanu, pafupifupi. Matenda achindoko anali atadya izo. Oh, inde, iye anali "Akukakhala ndi nthawi yopambana. Mtsikana wachikulire wamng'ono uyu anali woyera-wodzigudubuza." Usamachepsye kalikonse, mzanga.

200 Kodi iwe ukumudziwa Iye usikuuno? Kodi iwe unapulumutsidwa kwenikweni? Ine ndikukufunsa iwe, mu Dzina la Yesu. Ngati pali mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, muno usikuuno, yemwe sanapulumutsidwe, wobadwa mwatsopano, kodi inu mungakweze dzanja lanu? Ndikuti, "Ndipempherereni ine, M'bale Branham." Tsopano mutu uliwonse utaweramitsidwa. Inde, Mulungu akudalitseni inu, dona wamng'ono. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu, inu, inu, inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu. Kumbuyo kumbuyoko, inde, Mulungu akudalitseni inu. Mulungu adalitse kuwona mtima kwako, mnyamata, ine ndikukuwona iwe. Zodabwitsa. Manja twente kapena sarte mchipinda chaching'ono chino, osasinthika. Mzimu Woyera wakhala uli pano usikuuno, ukuyankhula ndi inu. Iye ali pano tsopano. Inu mukumufuna Iye. Bwanji osabwera? Kodi inu simubwera ku guwa ndi kudzagwada pansi? Ndikuti, "Ambuye Mulungu, ine ndikulandirani Inu ngati Mpulumutsi wanga wanga usikuuno. Ine ndikulandirani Inu tsopano, ndipo ine ndilandira Ubatizo wa Mzimu Woyera. Ine ndikuwufuna Iwo. Ine sindikusamala zomwe dziko likunena. Ine ndikulandirani inu tsopano. Inu munandilonjeza ine."

201 Ndipo, mvetserani, aliyense muno yemwe munagwira dzanja lanu, inu mwakhala mukumvetsera ku msonkhano uwu—misonkhano iyi. Palibe mmodzi muno angakhoze kubwera kwa Yesu kupatula Mulungu atamukoka iye. Ndi chiyani chikuchita zimenezo? Ndi chiyani chikupanga chokhumba chimenecho? Mulungu ali pano. Mulungu ali pano.

202 Mvetserani, mzanga, ngati Mulungu ati amve pemphero langa, ngati munthu, ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, ndipo mwawerenga manyuzipepala ndi magazini, ndi mabuku ndi maulamuliro, ndi kuyang'ana kumbuyo uko pa zithunzi zomwe iwo akugulitsa kuseri kwa chitseko usiku, za Mngelo wa Mulungu uja, akuyaka ndi Moto, Mmodzi yemweyo yemwe ine ndikumuwerenga apa mu chitsamba chonyeka, ndipo inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu, ndipo inu mukukhulupirira kuti Iye angamve pemphero langa, ndipo amva pemphero lanu ngati inu muti mupemphere, kodi inu mungafune kuti mudzuke pa

mpando wanu? Kodi inu muli nako kukhudzika kwenikweni koteroko? Bwerani kuno ndipo mudzaime pa guwa ili, ndi kuti, "M'bale Branham, ngati Iye ati atsegule maso a akhungu, Iye andikhulululukira machimo anga." Mulungu akudalitseni iwe, mnyamata, kudzipanga wekha kukhala woyamba kusuntha. Ndani amutsatire mnyamata uyu ku guwa ili?

203 Ine ndikufuna atumiki a nyumba ino abwere, mchipinda muno, bwerani kuno ku guwa miniti yokha, mlaliki aliyense. (Bwera, dona wamng'ono. Mulungu akudalitse iwe. Winawakenso tsopano.) Ine ndikufuna atumiki abwere kuno pamwamba pa nsanja, ngati inu mungathe.

204 Wochimwa, mzanga. Bwerani kuno, mnyamata. Mulungu akudalitseni inu. Bwerani komwe kuno ndi kudzagwada pansi apo pomwe. Mulungu akudalitseni inu, bwana, inu bwerani. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu. Winawakenso panga njira yako yobwera kuno ku guwa ndi kudzagwada pansi. Kodi inu mulibe Mulungu, mulibe Khristu, usikuuno, mu dziko lotalikirana?

Oh, inu mukuti, "Nthawi yatha pang'ono, ndipo anthu anga akuyembekezera."

205 Mtsikana wamng'ono wolumala akupanga njira yake. Manyazi pa inu anthu athanzi. Kodi ndinu mlendo kwa Mulungu usikuuno, wopanda Mulungu, wopanda Khristu, mukufa mu tchimo ndi manyazi? Kodi inu simubwera? Kodi inu mukhala mwamuna kapena mkazi mokwanira, ndi ulemu wamba wokwanira, kuti mudzuka ndi kunena kuti, "M'bale Branham, ine ndikubwera kuno, ine ndikufuna kuti ndigwire dzanja lanu ndi kudzagwada pansi apa pa guwa. Ine ndikufuna ndimulandire Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanga pakali pano"? Kodi inu mubwera?

206 Manja onse awo ali mmwamba, inu mukutanthauza kuti mundiuze ine, mwadziwa kuti mwaima pano mu Kukhalapo kwa Mulungu, mwadziwa kuti muli mu chikhalidwe ichi, ndipo mukukanabe kubwera ku guwa? Nanga bwanji ngati mtima wanu utakasiya usikuuno inu mukakafika kwanu? Bwanji ngati inu mutachita ngozi ndipo muli mchipatala ora limodzi kuchokera pano, magazi akutuluka kuchokera mthupi lanu, ndipo inu mukukuwa, koma palibe woti apemphere? Mulungu anati, "Ngati iwe undinyalanyaza Ine tsopano, Ine ndidzakuseka iwe mu tsoka lako." Kodi inu simubwera? Kwenikweni? Kodi iwe ukutanthauza kuti iwe unakhutitsidwa mokwanira kuti Mzimu Woyera uli pano, kuti iwe ukweza dzanja lako, ndipo kodi subwera ku guwa? Ndi chiyani mdziko chomwe chiri patsogolo pako?

207 Mulungu akudalitseni inu, bwana. Ine ndazindikira kuti inu ndinu munthu wodwala, nanunso, kuti inu mukubwera. Sichoncho inu? Inu mukudwala TB. Sichoncho inu? Iye

akuchizani inu pano pa guwa usikuuno. Ndinu mlendo kwa ine, koma ine ndikudziwa chimene inu muli ndi yemwe inu muli.

208 Mzimu Woyera unagwera mu msonkhano pamenepo. Ndipo Mngelo wa Mulungu uja wayima pa nsanja. Mwakhala muli mmisonkhano, inu mukudziwa chomwe izi zikutanthauza. Sichoncho inu?

Mwamunayo achiritsidwa usikuuno. Mulungu anayankhula basi pamene iye amadzuka kuchokera pamenepo.

209 Mulungu akudalitse iwe, mwana, zibwerani kumene. Kazibwerani, mukulira, ndipo maso odzaza misozi. Mulungu akudalitseni inu, mlongo, zibwerani kumene. Mulungu akudalitseni inu, zibwerani, dzagwadeni mozungulira guwa. Kodi inu simubwera?

> O Mwanawankhosa wa Mulungu, ine ndikubwera! Ine ndikubwera!
>
> Monga ine . . .

210 Mulungu akudalitse iwe, mnyamata wamng'ono. Ndizo zodabwitsa. Kodi winawakenso satero? Ena a inu achichepere kumbuyo uko tsopano, inu mwazikankhira izo kutali kwa nthawi yaitali. Iyi ndi nthawi yake. Ili ndi oralo.

> . . . solo kuchokera ku dontho limodzi lakuda,

211 Winawake awathandizire amayi kumbuyo uko ali ndi mwana ameneyo, winawake chonde. Iye akufuna kuti abwere ku guwa, mwamuna wake ali kuno. Ena a inu mumuthandizire mwanayo, kapena mumugwirizire mwanayo, mulole mayiyo abwere. Mulungu akudalitseni. Bwerani, amayi. Uko nkulondola. Iwo amusamalira wamng'ono wanuyo. Bwerani, mudzapange mayi weniweni wa Yesu Khristu ndi ana anu.

212 Mulungu akudalitseni inu, mlongo, izo ndi zabwino. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ndiyo njira yobwerera ndi kudzathetsa manjenje anuwo. Mwakhala mukukhala ndi vuto lamanjenje limenelo ndi zizolowezi ndi zinthu, izo zikusiyani inu mutayima pamenepo tsopano.

213 Mngelo wa Ambuye wayima pomwe pano pa nsanja iyi. Ngati inu mukundikhulupirira ine kukhala mneneri Wake, mumvere ndipo muchite zomwe ine ndikukuuzani inu tsopano, muwone ngati Izo siziri zolondola.

> Kuchotsa moyo wanga dontho limodzi lakuda,
> Kwa Inu, Magazi Anu . . . (Mulungu akudalitseni inu, mnyamata.) . . . amayeretsa malo aliwonse,
> O Mwanawankhosa wa . . . (Mulungu akudalitseni inu, amayi.) . . . Ine ndikubwera! Ine ndikubwera!

214 Kodi aliyense wa inu nonse mukufuna kuti mubwere? Mzimu Woyera ukundiuza ine kuti muli anthu ena angapo mmenemo. Mukhale owona mtima ndi Mulungu, simutero inu? Kodi inu mutaya chiyani, kuti muyende mubwere pamwamba pano pa guwa ndi kudzapemphera pang'ono? Inu mukapemphera kwinakwake. Ngati inu simupemphera pano, inu mudzakapemphera ku gehena. Mnyamata mwini chuma anakwezera maso ake. Tsopano, ngati inu mukukhulupirira, ngati inu mukukhulupirira Mawu a Mulungu, ndipo mukukhulupirira kuti ine ndikukuuzani Choonadi, ngati Mulungu watsimikizira Choonadi, pali amuna ndi akazi muno amene ayenera kukhala pa guwa ili pakali pano. Mzimu Woyera ukuyankhula, ukunena chomwecho. Bwerani! Mulungu akudalitseni inu, mlongo, ndinu basi mmodzi wa iwo. Bwerani. Mulungu akudalitseni inu. Bwerani tsopano, kulikonse kumene inu muli. Wamng'ono kapena wamkulu, bwerani.

215 Tiyeni tiyimirire. Anthu nonse inu mmipando yanu, imirirani pamene ife tikuyimba ndime imodzi ya iyi tsopano. Bwerani tsopano, fikirani pozungulira, tiyeni tipange njira yathu waku guwa. Inu ndinu wa tchalitchi, inu mukuti. Izo sizikukwanira. "Kupatula munthu atabadwa mwatsopano, iye sadzakhoza konse kulowa mu Ufumu." Kazibwerani tsopano.

Monga momwe . . . (Aliyense.) . . . Ine . . .

216 Kodi inu simutuluka? Kodi inu simubwera pansi mkanjira tsopano? Kazibwerani kuno ndipo mudzakumane nane pa guwa. [M'bale Branham wachoka pa guwa, zochuluka za zoyankhula zake sizikumveka—Mkonzi.] . . . ? . . . Mulungu akudalitseni inu . . . ? . . . mmodzi winanso.

Monga momwe . . . (Mulungu akudalitseni inu, M'bale Joe . . . ? . . . )
Kuti monga Magazi Anu anakhetsedwa . . . ? . . .
. . . monga ine ndiri . . . ? . . .
. . . wa Mulungu, ine ndikubwera! Ine ndikubwera!

Monga ine ndiriri, ndipo osadikira,
Kuchotsa moyo wanga (Ndi angati?) za dontho limodzi lakuda,
Kwa Inu, Yemwe Magazi Ake angayeretse banga lirilonse,
O Mwanawankhosa wa Mulungu, ine . . .

217 Ndi angati muno akuti, "M'bale Branham mundipempherere ine, ine sindiri wolimba mtima mokwanira kuti ndibwere. Ine ndikufuna kuti inu mundipempherere ine"? Kwezani dzanja lanu tsopano pamene ife tikuyiyimba iyo kachiwiri. Pitirirani nazo. Kwezani dzanja lanu, munene kuti, "M'bale Branham, mundipempherere ine."

Mulungu akudalitseni inu, mlongo . . . ? . . . Mzimu Woyera wabwera wamoyo . . . ? . . . Ine ndinawona . . . ? . . . wanu . . . ? . . . oyitanidwa ndi Mzimu Woyera . . . ? . . . kuyitanira kuguwa . . . ? . . .

53-0328 Israeli Ndi Mpingo #4
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org